


KUKHAZIKITSIDWA ¹

 ...ine ndikumverera bwino kumva zimenezo, izo ndi zabwino. Chabwino, zimakhala chomwecho nthawizonse, monga ine ndanenerapo kale, “Ine ndinali wokondwa pamene iwo anati kwa ine, “Tiyeni tipite kunyumba ya Ambuye.”” Ine ndikukhulupirira Davide ananeno zimenezo nthawiina, “Tiyeni tipite kunyumba ya Ambuye.” Ine sindikudziwa malo abwino aliwonse oti nkukakhalako, sichoncho inu, kuposa kukhala mnyumba ya Ambuye.

² Tsopano, usikuuno, ife tiri ndi abwenzi ena pano amene achokera komwe ku Georgia. Iwo mwinamwake akhala akuyendetsa kupita kumusi tikatsiriza—tikatsiriza kudya chakudya cha masana usikuuno. Ndiyeno ife ti...Ena a iwo akuchokera kumusi uko, ine ndikudalira kuti mutsalira. Ndipo zipinda zimene ife tiri nazo ndi zotseguka kwa inu.

³ Ndipo kenako Lachitatu usiku ife tidzakhala tikupitirira, pa kuphunzira, ndipo kenako, Ambuye akalola, Lamlungu lotsatira kenanso.

⁴ Ndipo kenako Chautauqua adzayamba pa sikisi. Chotero nonse amene mwakonzekera tchuthi chanu, ife tikuyembekeza kuti tikakhala ndi nthawi yopambana, yodabwitsa ku Chautauqua. Kumeneko ndi kumene ife nthawizonse timakhala ndi nthawi yopambana yotero. Si magulu aakulu kwambiri, omwe nthawizina timakhala nawo...Umo mumakhala pafupifupi...Ine ndikuganiza ife tikhiza kuyikamo teni sauzande mmenemo, mophweka. Koma, kawirikawiri, chaka chatha ine ndikuganiza ife tinali ndi pafupifupi seveni sauzande, chinachake monga choncho. Malowo anali atadzaza, koma panali malo ambiri oti nkuimapo. Ndi mipando imene iwo akanakhoza kuyiyala mpaka panja. Ndipo chotero ife tikuyembekezera zimenezo.

⁵ Ndipo wokondwa kuwona ambiri a abale athu otumikira mkati muno. Ine ndikulephera kuti ndiganizire dzina lake apa, wamishonare, M'bale Humes ndi Mlongo Humes, kodi ndinu mwakhala pomwe apa, ndi ana, ndife okondwa kukhala nawo iwo, amishonare. Enawo, M'bale Pat, M'bale Daulton, ndi, oh, ambiri basi, M'bale Beeler. Ndipo ndinamuwona M'bale Collins mphindi pang'ono zapitazo. Ndipo, oh, izo zingakhale zovutirapo kuwatchula iwo onse. Koma ndife okondwa kwambiri kukhala nanu inu mnyumba ya Ambuye usikuuno. M'bale Neville wofunika kwambiri uyu wakhala kumbuyo kwanga kuti azipemphera nane pamene ife tikhale tikuphunzitsa Mawu. Charlie, ndine wokondwa kukuwona iwe ndi Mlongo Nellie pano usikuuno, ana. Ichi ndi...ndipo

kuphunzitsa kwa Baibulo kawirikawiri kumakhala...Inde, M'bale Welch, ine basi...ndimakuyang'anayang'ana iwe, ine ndakuwona iwe wakhala kumbuyo uko tsopano.

⁶ Kuphunzitsa kwa Baibulo kawirikawiri kumakhala kowopsya pang'ono, pang'ono, inu mukudziwa, zimakhala ngati ukuyenda pa ayesi wopyapyala, ife timazitcha izo. Koma ife timangomverera kuti mwinamwake, pamene tafikapa ndipo pa nthawi ino, izo zingakhale zabwino kuti ndiwufikitse a—mpingo ku chimene ine ndikuganiza, ku—kumvetsa kwathunthu, kwa pamalo ake, a chimene ife tiri mwa Khristu Yesu. Ndipo nthawizina ine ndimaganiza kuti kulalikirira ndi chinthu chophambana, koma ine ndimakhulupirira nthawizina, M'bale Beeler, kuti kuphunzitsa kumapita kudutsa pamenepo, iko mwabwino...makamaka kwa mpingo.

Tsopano, kulalikirira kawirikawiri kumamugwira wochimwa, kumamubweretsa iye panso pa kutsutsika ndi Mawu. Koma kuphunzitsa kumamuyika munthu pamalo a chimene iye ali. Ndipo ife sitingathe molondola kukhala ndi chikhulupiriro mpaka ife titadziwa malo athu a chimene ife tiri.

⁷ Tsopano, ngati United States, wa dziko labwino ili kuno, atanditumiza ine ku Russia, ngati kazembe wa fuko lino, ku Russia, ndiye ngati iwo movomerezeka atanditumiza ine ku Russia, mphamvu zonse zimene United States ali nazo zikakhala pa nsana panga. Mawu anga akakhala chimodzimodzi basi ngati a United States, ngati ine nditavomerezedwa kukhala kazembe.

⁸ Ndiyeno ngati Mulungu watitumiza ife kudzakhala akazembe Ake, mphamvu zonse zimene ziri Kumwamba, zonse zimene Mulungu ali, Angelo Ake onse ndi mphamvu Zake zonse ziziyima kumbuyo kwa mawu athu ngati ife tiri odzozedwa molondola, atumiki otumizidwa kwa anthu. Mulungu akuyenera kulemekeza Mawu, pakuti Iye mwaulemu analemba, kuti “Chirichonse chimene inu mudzamanga padziko lapansi, chimenecho Ine ndidzachimanga Kumwamba. Chirichonse chimene inu mudzachimasure pa dziko lapansi, chimenecho ine ndidzachimasure Kumwamba. Ndipo ndikukupatsa iwe mafungulo aku Ufumu.” Oh, malonjezo opambana oterowo Iye anawapereka kwa Mpingo!

⁹ Ndipo ine ndiri, litadutsa tsiku linalo...Ambiri a inu, ine ndikuganiza, munali pano mmawa uno kudzamva pamene ine ndimayesetsa kuti, mwanjira yanga yodzichepetsa, yophweka, ndimafotokoza ma—masomphenya amene ine ndinawawona a Kumwamba.

¹⁰ Ine mwanjira iliyonse sindingayesere kukaikira chirichonse chimene aliyense angandiuze ine chimene Mulungu anawauza iwo. Ine ndikhoza kukhulupirira icho ngakhale ine ndisanachiwone icho mu Lemba, ine ndingafunebe kuti ndikhulupirire mawu a m'bale ameneyo. Ine—ine ndikhoza

kungokhalabe ndi Baibulo, komabe ine ndikhoza kukhulupirira kuti mwinamwake m'baleyo sanazimvetse izo mwanjira inayake, kuti iye anangozisokoneza izo pang'ono. Ndipo komabe ine ndingamukhulupirire iye—iye kuti ndi m'bale wanga.

¹¹ Ndipo ngati pali chirichonse chimene chikutentha mu mtima mwanga, ndipo ine ndikudalira kuti icho sichidzachoka mu zaka zanga zimene zikubwerazi, kuti ine sindidzaiwala konse chimene chinachitika Lamlungu lapitali mmawa, ngati sabata. Ichu chachita chinachake kwa ine chimene chasinthu moyo wanga. Ine—ine sindikuwopa. Ine—ine ndiribe mantha amodzi a imfa. Imfa ilibe mantha konse. Ndipo iyo—iyo siingatero kwa inu ngati mutangomvetsetsa. Tsopano, mwinamwake ngati... Inu mungayenere kukhala ndi chokuchitikirani kuti mudziwe izo, chifukwa palibepo njira yozifotokozera izo. Inu simungathe kuwapeza mawu, chifukwa iwo mulibemo mu dikishonare ya Chirengezi, kapena osati mu dikishonare iliyonse, chifukwa izo ziri mu Muyaya; kunalibeko dzulo, kunalibeko mawa, zonse zinali za lero. Ndipo sizinali “ine ndikumverera bwino,” ndipo ora kuchokera pamenepo, “ine sindikumverera bwino kwambiri,” ndipo ora linalo, “ndikumverera bwino kenanso.” Zimakhala za lero nthawi zonse. Mukuona? Sizimaleka nkomwe, basi zimangokhala mtendere wa ulemelero umenewo basi, chinachake.

¹² Ndipo kumeneko sikungakhaleko tchimo, sikungakhale nsanje, sikungakhale matenda, uko—sikungakhale chirichonse chokafika ku gombe la Kumwamba limenelo. Ndipo ngati ine ndingakhale ndi mwayi wonena izi, chimene, mwinamwake ine sindikhala nawo. Ngati ine sinditero, ndiye ine ndikupemphera Mulungu andikhululukire ine. Koma ngati ine ndingakhale nawo mwayi, ndipo iwo unali woti Mulungu anandilola ine kuti nditengedwere mmwamba kuti ndikawone chinachake, ine ndingaloze za Mmiyamba moyamba. Ndiyeno ine ndikukhulupirira, wina mu Baibulo, dzina lake, ine ndikukhulupirira anali Paulo, amene anatengedwera mmwamba mu Miyamba mwachitatu. Ndipo ngati munali mwa ulemelero chonchi m'Miyamba moyamba, m'Miyamba mwachitatu mungakhale motani? Nzosadabwitsa iye sanayankhule za izo kwa zaka fortini! Iye anati iye samadziwa kaya iye anali mu thupi kapena kunjwa kwa thupi. Ndi mtumwi wamkulu ameneyo, sikuti ndikufuna kugawana naye yake—yake—ofesi yake, kapena sikuti ndikuyesera kuti tidzipange tokha kukhala chirichonse monga chimene iye anali, koma ine ndikhoza kunena limodzi naye, ine sindikudziwa kaya ndinali mthupi ili kapena kunjwa kwa thupi. Chinthu chokhacho, izo zinali zenizeni basi chimodzimodzi monga mmene ine ndikuyang'anira pa inu.

¹³ Ndipo ine nthawizonse ndakhala ndikudabwa ngati ndizidzadutsa ndi kuwona mtambo waung'ono ukuyandama, mzimu, ndikuti, “Apo akupita m'bale ndi mlongo, ameneyo ndi

Charlie ndi Nellie. Ameneyo ndi M'bale ndi Mlongo Spencer akupita pamenepo.” Zimenezo nthawizonse zinkandidodometsa ine. Ngati maso anga adzakhala ali mmanda, akuvunda, akuwola, ngati makutu anga sadzakhala kuno kuti ndizidzamverera, ndipo ngati magari anga onse abwerera kwawo ndipo awawumitsa iwo, ndipo iwo ali mmadzi kapena mu nthaka, ndipo ubongo wanga woganizira, makhungu a ubongo anga onse apita, ndiye ine ndingadzakhale motaninso kuposa kungokhala kamzimu ndikuyandama yandama? Ndipo zimenezo zinkandidandaulitsa ine. Mmene ine ndingadzakondere kudzati, “Moni, M'bale Pat, oh, wokondwa kwambiri kukuwonani inu! Moni, M'bale Neville, mmene ine ndikufunira nditakuwonani inu!” Koma ine ndinaganiza, “Chabwino, ngati ine ndidzakhale ndiribe chirichonse chopenyera, kamwa iliyonse yoti ndizidzayankhulira nayo, iyo yavunda, iyo ndi fumbi, ine ndidzatha bwanji kudzati, ‘Moni, M'bale Pat,’ ‘Moni, M'bale Neville,’ kapena zina zotero, ‘Moni, Charlie?’”

¹⁴ Koma tsopano ine ndadziwa kuti uko kunali kulakwitsa. Pakuti munalembedwa mu Malemba, chimene ine ndikunena kuti sizikutsutsana, “Pakuti ngati msasa wa pansu pano upasuka, ife tiri nawo wina umene ukudikirira,” msasa wina umene uli nawo maso, makutu, milomo, ubongo woganizira. “Ngati msasa wa pa dziko lapansi uwu udzapasuka!” Iye ali nalo thupi limene ine ndikhoza kulikhudza, ndikhoza kuyankhula.

¹⁵ Ndipo tsopano izo zangobwera kumene kwa ine, pompano, kuti Mose anali atafa ndipo anakhala mmanda osadziwika kwa zaka eyiti handiredi, ndipo Elisha anali atapita Kumwamba zaka faifi handiredi mmbuyo mwake, koma pa Phiri la Chivalitsiro iwo anapezeka akuyankhulana ndi Yesu.

¹⁶ Samuele atatha kufa kwa pafupifupi pakati pa zaka firii ndi faifi, ndipo mfiti ya ku Endori inamuitanitsa iye, ndipo iye anadzagwa pamaso pake, ndipo iye anati, “Iwe wandinyenga ine, chifukwa iwe ndi Sauli, iwemwini.” Iye anati, “Chifukwa ine ndikuwona milungu!” Iye anali wachikunja, inu mwaona. “Ine ndikuwona milungu ikuwuka.”

¹⁷ Ndipo Sauli anali asanamuwone iye apobe, ndipo iye anati, “Iye akuwoneka motani? Tamufotokozani iye kwa ine.”

Anati, “Iye ndi wochepa thupi, ndipo ali ndi chovala pa phewa pake.”

¹⁸ Anati, “Ameneyo ndi Samuele, mneneri, mubweretse iye kuno pamaso panga.” Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzindikire kuti Samuele sanataye umunthu wake uliwonse. Iye anali akadali mneneri. Iye anamuza Sauli ndendende zimene zikanadzachitika tsiku lotsatira.

¹⁹ Chotero, inu mukuona, imfa siimatimalizitsiratu ife kwathunthu monga mmene ife timalirira ndi kuisima ndi kumadandaula pa manda. Iyo imangotisinthira malo athu

okhalako. Iyo imangotitengera ife malo ndi malo. . . Usinkhu ndi chiyani? Ngati ine ndingakhale ora lina limodzi, ine ndikhoza kukhala moyo kuwaposa anthu a usinkhu wa zaka sikisitini ambiri, ine ndikhoza kukhala moyo kumuposa munthu wa usinkhu wa zaka faifi. Usinkhu si kanthu. Ife tinadzangoikidwa kuno kwa cholinga, kuti tidzachite chinachake.

²⁰ Chabwino, tsopano, ambiri a azimayi owoneka bwino amene akhala pano awa, ena a iwo a usinkhu wa zaka sikisite kapena sevente zakubadwa, akhoza kunena kuti, “Chabwino, ine ndachita chiyani, M’bale Branham?” Inu mwalera ana anu. Inu mwachita zimene mumayenera kuti mudzachite.

²¹ Mwinamwake Bambo wina wokalamba wakhala apa, akuti, “Chabwino, ine ndimafafaniza minda, ine ndimachita *izi*. Ine sindinalalikirepo.” Koma inu munangochita basi chimene Mulungu anakutumizirani inu kuti mudzachite. Malo anu aliko.

²² Ndikuyankhula ndi dokotala wokalamba, dzulo, mmodzi wa dokotala mzanga, abwenzi, usinkhu wa zaka eyite chakuti zakubadwa. Ndipo mlamu wake wamkazi ali pano mu tchalitchi usikuuno, ndipo iye anangokhala, wodandaula pang’ono za iye. Ndipo ine ndinapita kuti ndikamuwone iye. Ndipo mwamsanga pamene ine ndinayamba kuyankhulana naye iye, iye anachangamuka, anandiuza ine za ulendo wokusaka umene iye anali nawo zaka zambiri zapitazo kumtunda uko mu Colorado, dziko lomwelo kumene ine ndimakasakako. Ali wochangamuka basi ndipo akuwala! Ndipo ine ndinati, “Dokotala, inu mwakhala mukugwira ntchito nthawi yaitali bwanji?”

²³ Iye anati, “Pamene iwe unkayamwa.” Ndipo mmusi mwenimweni ine ndinati. . . “Ndipo nthawi zambiri,” iye anati, “Ine ndimagwira ntchito, kumatenga ngolo yanga, ine ndimaika zikwama za chishalo changa pa kavalo wanga. Ine ndimatenga kachikwama kakang’onoko ndipo nkumayenda.”

²⁴ Ndipo ine ndinati, “Inde, kumatsika mmphepete mwa gombe la mtsinje, thuu koloko mmawa, muli ndi tochi yanu, kuyesera kuti mukapeze nyumba imene mwana anali ndi kupweteka kwa mmimba kapena mayi amene ali mu ululu wa kubala.”

“Uko nkulondola.”

²⁵ Ndipo ine ndinati, “Inu mukudziwa, adokotala, ine ndikukhulupirira, kudutsa mzere wolekanitsa uwu apa, pakati pa chivundi ndi chisavundi, Mulungu ali nawo malo a madokotala abwino okalamba amene anagwira ntchito monga chomwecho.”

²⁶ Misozi yaikulu inabwera mmaso mwake ndipo anayamba kulira, iye anakwezera mmwamba manja ake ofooka ndipo anati, “M’bale, ine ndikukhulupirira chomwecho.” Kutsidya linalo, Mulungu amaweruzo solo ya munthu, chimene iye ali.

27 Kenako ndinamupatsa iye Lemba lokhutitsa ili. Nthawi zambiri, mmayenda mminda ya mdima ya matope iyo usiku, kuyesetsa kuti mukamuthandize winawake, mwinamwake osapezapo ndalama mukachita zimenezo, koma izo ziri bwino. Ine ndinati, “Yesu anati Mmalemba, ‘Odala ali achifundo, pakuti iwo adzalandira chifundo.’” Ndipo izo ndi zoon.

28 Ndipo usikuuno ife tikufuna kuti tiwukhazikitse mpingo, mu maphunziro atatu awa, ngati Mulungu aroleza, motani ndipo kodi tiziyang’ana chiyani, chimene ife tiri. Ife tiyambira pa mutu wa 1 wa Bukhu la kalata ya Paulo kwa Aefeso. Ndipo ife titenga mitu itatu yoyambirira mu maphunziro athu atatu otsatira, kuyesetsa kutenga mutu pa usiku, ngati ife tingathe. Usikuuno, Lachitatu, ndi Lamlungu lotsatira mmawa. Aefeso, mutu wa 1. Tsopano pamene ife tikuwerenga limodzi, ine ndikufuna kuti ndinene ichi, kuti Bukhu ili la Aefeso mwangwiro limafanana ndi Yoswa wa Chipangano Chakale. Aefeso, Bukhu la Aefeso.

29 Tsopano, kumbukirani, ngati zitachitika kuti ife tachokapo pang’ono, ku chiphunzitso chanu, mungotikhulukira ife ndipo mupirire nafe pang’ono. Ife tisanatsegule ilo, tiyeni timufunse Iye kuti atithandize ife, pamene tikuweramitsa mitu yathu.

30 Ambuye, ife tikuyandikira Zolembedwa Zanu zoyera ndi zopatulika, chimene Izo ndi zotetezeka kwambiri kuposa miyamba yonse ndi dziko lapansi. Pakuti ife timawerenga mu Mawu awa, otchedwa Baibulo, kuti “Kumwamba ndi dziko lapansi zonse zidzapita, koma Mawu Anga sadzalephera konse.” Ndiye, pa ora laulemu lino limene ine ndikubwera pa guwa ili usikuuno, pamaso pa ogulidwa ndi Magazi Anu, achivundi odula okonededwa awa amene akhala pano usikuuno, kutenga chiyembekezo chaching’ono chirichonse chimene iwo angathe, kuti agwiritsitsebe chifukwa cha Kuwala uko kumene kuli nkudza. Mulole izo zikhale zokwanira kwambiri, usikuuno, kuti wokhulupirira aliyense muno awone malo ake, ndipo aliyense amene sanabwere panobe mu chiyanjano chachikulu ichi, akangamire Ufumu, Ambuye, ndipo adzagogode pakhomo kufikira Woyang’anirayo atatsegula chitseko. Perekani izi, Ambuye.

31 Ife tikuwerenga apa pamene Baibulo ili liribe kutanthauzira kwamseri. Mulungu, musalole kuti ine wantchito Wanu kapena wantchito wina aliyense adzayesere konse kudzaika kutanthauzira kwawo kwawo ku Mawu. Tiloleni ife tingowerenga Iwo ndi kuwakhulupirira Iwo, mmene Iwo analembedwera. Ndipo makamaka ife azibusa a nkhosa, ife abusa amene tsiku lina tidzakasonkhana uko mu Dziko la ulemelero lija ndi nkhosa zapang’ono, ndipo tidzakaima mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu ndipo tidzawuwona m’badwo umenewo ukutulukira, wa Paulo, ndi wa Petro, ndi wa Luka, ndi Marko, ndi Mateyu, ndi onse awo, ndipo tidzawawona iwo akuweruzidwa kumeneko ndi magulu awo. Mulungu, perekani

kuti ine ndidzathe kudzaika zikho teni milioni pa mapazi Anu pamene ine modzichepetsa ndizidzakwawira chokwera ndi kudzaika manja anga pa mapazi Anu ofunika, ndikuti, “Ambuye, iwo ndi Anu.”

³² O Mulungu, tidzazeni ife mwatsopano ndi Mzimu Wanu, ndipo ndi chikondi Chanu ndi ubwino Wanu. Ndipo mulole ife, monga wandakatulo anafotokozera mu nyimbo zaka zambiri zapitazo, “Wokonedwa Mwanawankhosa wakufa, Magazi Anu ofunikira sadzataya mphamvu yake, mpaka Mpingo wonse wowomboledwa wa Mulungu udzapulumutsidwe kuti usadzachimwenso. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, mwa chikhulupiriro, ine ndinawona mtsinje uja umene mabala Anu osefukira amapereka; chikondi chowombola chakhala chiri nkhani yanga, ndipo idzakhala mpaka ine ndidzafe. Kenako mu nyimbo yochirimika, yokoma,” iye akupitirira kumati, “Ine ndidzaimba mphamvu Yanu yopulumutsa; pamene lirime losauka losayankhula bwino ili, lachibwibwi lidzagone chete mmanda.” Zikadzatero, manda sadzagwira imfa iliyonse ya ana Anu. Iyo ndi malo opumulirako chabe, kapena malo obisalako, kumene chivundi ichi chiti chidzakavale chisavundi.

³³ Mulole ife usikuuno tiziwone izi, Ambuye, pambalambanda, munga izo zinaperekedwera kwa ife mu Mawu. Tipatseni ife kumvetsa. Ndipo mukatiike ife, Ambuye, pa malo athu a ntchito, kuti ife tikakhoze kutumikira mokhulupirika mpaka Inu mudzabwere. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, ndi chifukwa cha Iye. Amen.

³⁴ Tsopano, Bukhu la Aefeso, monga mmene ine ndimangonenera, ine...mwa kuganiza kwanga, ndi limodzi la Mabukhu opambana kwambiri a Chipangano Chatsopano. Ilo limakatsiya ife, kumene Chikalvini chimakayenda pa nthambi imodzi, ndipo Chiarminia chimakayenda pa nthambi inayo, koma Bukhu la Aefeso limazibweretsa izo pamodzi ndi kudzawuika Mpingo pamalo ake.

³⁵ Tsopano, ine ndazifanizitsa izo ndi Yoswa. Ngati inu mungazindikire, Israeli anatulutsidwa kuchokera ku Igupto, ndipo panali magawo atatu a ulendo wawo. Gawo limodzi, linali kuchoka ku Igupto. Gawo lotsatira, linali mchipululu. Ndipo gawo lotsatira, linali Kenani.

³⁶ Tsopano, Kenani samaimira m’badwo wa Zakachikwi. Iye amangoimira m’badwo wa mgonjetsi, kam’badwo kogonjetsa, chifukwa mu Kenani iwo amapha ndi kuwotcha ndipo amalanda mizinda. Ndipo simudzakhala imfa mu Zakachikwi.

³⁷ Koma chinthu china chimene iye amachita, iye amabweretsa kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro, iwo atatha kumukhulupirira Mose ndi kuchoka ku Igupto. Kuyeretsewa, kumatsatira pansa pa Lawi la Moto ndi chitetezero cha

mwanawankhosa wa nsembe mu chipululu. Ndipo kenako nkudzalowa mdziko limene linali litalonjezedwa.

³⁸ Tsopano, kodi dziko lolonjezedwa kwa wokhulupirira wa Chipangano Chatsopano ndi liti? Lonjezolo ndi Mzimu Woyera. “Pakuti kudzachitika mmasiku otsiriza,” Yoweri 2:28, “kuti ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa thupi lonse. Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera. Ndipo pa antchito Anga ndi adzakazi Anga ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga, ndipo iwo adzanenera. Ine ndidzawonetsa zodabwitsa mmiyamba mmwamba. Ndi mdziko lapansi, malawi a moto, ndi utsi, ndi mame.” Ndipo Petro anati, pa Tsiku la Pentekoste, atatenga phunziro lake ndipo nkumalalikira, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro,” kuchotsa, kukhululuka, kuchotsa zolakwa zammbuyo zonse.

³⁹ Kodi inu munazindikira, Yoswa, iwo asanawoloke Yordani, Yoswa anati, “Mupite pakati pa msasawo ndipo mukachape zovala zanu ndipo mukadziyeretse mmodzi aliyense wa inu, ndipo musakalole mwamuna aliyense akagone ndi mkazi wake, pakuti mmasiku atatu inu muwona Ulemelero wa Mulungu.” Mukuona? Iyo ndi—iyo ndi ndondomeko yokonzekera kukalandira lonjezolo. Tsopano, lonjezo kwa Israeli, linali, Mulungu anamupatsa Abrahamu lonjezo la dziko, la Palestina, ndipo ilo linali loti lidzakhale cholowa chawo kwa nthawizonse. Ndipo iwo anali woti azikhala mdziko ili nthawizonse.

⁴⁰ Tsopano, iwo anabwera mmagawo atatu, akubwera ku dziko lolonjezedwa ili. Tsopano penyani, izo zikufanizidwa mwangwiro mu Chipangano Chatsopano.

⁴¹ Tsopano izi, monga ine ndanenera, zimatsutsana ndi kuganiza kwina kwa inu. Ena a inu anthu ofunikira achi Nazarene, Church of God, ndi ena otero, musalole kuti izi zikupwetekeni, koma mungowona izo mwatcheru ndipo muwone zomira zake. Mupenye ndipo muwone ngati malo aliwonse sakugunda mwangwiro basi.

⁴² Kunali magawo atatu a ulendowo, ndipo alipo magawo atatu a ulendo uno. Pakuti, ife timalungamitsidwa mwa chikhulupiriro, kukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, kulisiya dziko la Igupto, kutulukamo. Ndipo kenako nkudzayeretsedwa kudzera mu kupereka kwa Magazi Ake, kusambitsidwa ku machimo athu, ndi kudzakhala amwendamnjira ndi alendo, kumadzinenera kuti tikufunafuna dziko, mzinda umene ukubwera, kapena lonjezo.

⁴³ Chomwechonso anatero Israeli mu chipululu, apaulendo, opanda malo opumulirako, akuyenda usiku ndi usiku, akutsatira Lawi la Moto, koma potsiriza anadzafika ku dziko lolonjezedwa kumene iwo anadzakhazikikako.

⁴⁴ Kumeneko ndi kumene wokhulupirira amadzafikako. Poyamba iye amabwera pozizindikira kuti iyeyo ndi wochimwa;

kenako iye amadzalekanitsidwa ndi madzi, kusambitsa kwa madzi, mwa Magazi, ndipo... kapena kusambitsa kwa madzi mwa Mawu, kani, kukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu. Ndiye, polungamitsidwa mwa chikhulupiriro, iye amadzakhala wotenga nawo, ndipo amakhala pa mtendere ndi Mulungu, kudzera mwa Khristu, kubatizidwa kulowa mu Dzina la Yesu Khristu, kukamulowetsa iye mu ulendo. Inu mukumvetsa zimenezo? Kukalowa mu ulendo! Kenako iye amadzakhala wapaulendo ndi mwendamnjira. Iye amakhala ali pa ulendo wake wopita ku chiyani? Lonjezo limene Mulungu anapanga.

⁴⁵ Israeli anali asanalandirebe lonjezo, koma iwo anali ali pa ulendo wawo. Ndipo musananyamuke... Chonde tamvetserani. Pamenepo ndi pamene inu, a Nazarene ndi a Pilgrim Holiness, ndi ena otero, munalepherera. Chifukwa, Israeli, pamene iwo anadzafika pamalo amenewo, a Kadesh-Barnea, pamene azondi anapita uko ndikuti, “Dzikolo ndi labwino,” koma ena a iwo anabwerera ndikuti, “Ife sitingathe kulitenga ilo, chifukwa mizindayo ili ndi malinga, ndi zina zotero.” Koma Yoswa ndi Kalebu anaimirira, ndipo anati, “Ife ndi oposa kuthekera kulitenga ilo!” Chifukwa mfundo zawo zinali zitalembedwa kale ndi kusainidwa, iwo ankakhulupirira mu ntchito ziwiri za chisomo, kulungamitsidwa ndi kuyeretsedwa, ndipo sakanatha kusunthira mtsogolo mulimonse. Ndipo, mvetserani, kam’badwo konseko kanakathera mu chipululu. Koma awiri amene anakalowa mdziko lolonjezedwalo ndipo anabweretsako umboni wakuti ilo ndi dziko labwino, “ndipo ife tinali othejera kulitenga ilo, chifukwa ilo linali lonjezo la Mulungu.” Ndiye mmalo moti anthuwo azipitirira patsogolo, kukalandira Mzimu Woyera, kukayankhula ndi malirime, kukalandira mphamvu ya Mulungu, ubatizo wa Mzimu Woyera, zizindikiro, zodabwitsa, zozizwitsa, iwo anamverera kuti izo zikhoza kusokoneza mwambo wawo wa chiphunzitso. Ndipo chinachitika nchiyani kwa izo? Anafera mdzikolo! Uko nkulondola!

⁴⁶ Koma okhulupirira, onga ngati Kalebu ndi Yoswa, amene amapitirira kupita ku lonjezo, iwo anasamukira mpaka ku dzikolo, ndipo anakalitenga dzikolo, ndipo anakakhazikika mdzikolo, ngati cholowa. Ndipo ife sitimaimira konse pa kulungamitsidwa, kuyeretsedwa. Tiyeni tipitirire mpaka ku ubatizo wa Mzimu Woyera. Tiyeni tisaimire pa kukhulupirira Ambuye Yesu, kungobatizidwa. Tiyeni tisaimire chifukwa Iye anatiyeretsa ife ku moyo wa tchimo. Koma tsopano ife tikakamire mpaka tikafike ku malowo, ku lonjezo la ubatizo wa Mzimu Woyera. Pakuti Petro anati, pa Tsiku la Pentekoste, “Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.”

⁴⁷ Chotero, Aefeso apa akutiika ife monga Yoswa, kutiika pamalo. Inu mukuzindikira, Yoswa, atawolokera ku dzikolo,

ndipo nakatenga dzikolo, kenako iye analigawaniza dzikolo. “Efremu *apa*, Manasse *apa*, ndipo uyu *apa*, Gadi *apa*, Benjamin *apa*.” Iye analigawaniza dzikolo.

⁴⁸ Ndipo zindikirani! Oh, ichi chikutenthetsa mitima yathu! Aliyense wa amayi achi Hebri amenewo, akubereka ana amenewo, iye amawayankhula malo enieniwo, mu ululu wake wakubala, kumene iwo akanati adzaikidwe mu dziko lolonjezedwalo. Oh, ndi phunziro lalikuru! Ngati ife tingapite mmenemo mwatsatanetsatane, zimene zingatenge maora pambuyo pa maora. Tsikulina ife tikadzakonza tchalitchi chathu, ine ndikufuna kuti ndidzangobwera ndi kudzatenga mwezi wathunthu kapena iwiri, basi kudzangokhala mmenemo. Penyani pamene iwo, aliyense wa amayi amenewo, pamene iye ankaitana, “Efremu,” pamene iye anali mu kubereka, anamuika iye pamalo amene mapazi ake anali ataponda mmafuta. Basi ndendende aliyense wa iwo paliponse pamene iwo anali!

⁴⁹ Ndipo Yoswa, asakudziwa izi, koma mwa kudzoza, motsogozedwa ndi Mzimu Woyera, atatha kukalowa mdziko lolonjezedwalo, anamupatsa munthu aliyense lonjezo lake, ndendende chimene Mzimu Woyera unalonjeza kudzera mu kubadwa kumbuyo uko.

⁵⁰ Mmene Mulungu wawaikira ena mu mpingo, kudzera mu ululu wakubala! Oh, iwo amakhala opambana nthawizina. Pamene mpingo ukubuula pansi pa kuzunzika kwa dziko lakunja, kukhulupirira pa Ambuye Yesu, kuti lonjezo la Mzimu Woyera ndi lenileni basi kwa ife monga ilo linali kwa Pentekoste, mmene iwo ankabuulira ndi kulira pansi pa ululu wakubala! Koma pamene iwo abadwa, ndipo nkubadwira pa malo awo mu Ufumu wa Mulungu, ndiye Mzimu Woyera umawaika mu mpingo, ena atumwi, ena aneneri, ena aphunzitsi, ena abusa, ena avangeri. Ndiye Iye amapereka mmenemo, kuyankhula ndi malirime, kutanthauzira kwa malirime, chidziwitso, nzeru, mphatso za machiritso, mitundu yonse ya zozizwitsa.

⁵¹ Kumene kuli mpingo... Tsopano ichi ndi cholinga changa chochitira izi. Mpingo nthawizonse ukumayesetsa kutenga ngodya ya winawake. Koma musamachite zimenezo. Inu simungalime chimanga pa ngodya ya Efremu, ngati inu muli Manasse. Inu mukuyenera kutenga malo anu mwa Khristu, kuwatenga iwo pamalo ake. Oh, izo zimazama ndi kukhuthala pamene ife tidzalowe umu, mmene Mulungu amamuikira wina mu mpingo kuti aziyankhula mmalirime, wina... Tsopano, ife taphunzitsidwa nthawi zambiri, “ife tonse tikuyenera kuyankhula ndi malirime.” Zimenezo nzolakwika. “Ife tonse tikuyenera kuchita izi.” Ayi, ife tisatero. Iwo onse sankachita chinthu chimodzi. Aliyense anali... .

⁵² Aliyense, dzikolo linaperekedwa ndi kugawidwa mwa kudzoza. Ndipo, aliyense, ine ndikhoza kutenga Malemba ndi

kuwonetsa izo kwa inu ndendende, kuti iye anakawayika iwo pa malo amene iwo ankayenera kukhalapo, pamalo awo, mmene mafuko awiri athekawo anali woti akakhale kutsidya kwa mtsinje, mmene amayi awo ankalirira zimenezo mu kubadwa kwawo, ndi mmene malo aliwonse ankayenera kukhalira.

⁵³ Ndipo tsopano inu mutatha kulowa, zimenezo sizikutanthauza kuti inu simumakhala ndi nkondo. Inu mukuyenera kuti muzimenerabe inchi iliyonse ya malo amene mwaimapowo. Chotero, mwaona, Kenani sankaimira Kumwamba kwakukulu, chifukwa kumakhala nkondo ndi mavuto ndi kuphana ndi kumenyana, ndi zina zotero. Koma iye ankaimira ichi, kuti kumayenera kukhala kuyenda kwangwiro.

⁵⁴ Pamenepo ndi pamene mpingo ukulephera lero, pa kuyenda kumeneko. Kodi inu mukudziwa kuti ngakhale khalidwe lanu lomwe likhoza kumugwetsa winawake kuti asachiritsidwe? Kupanda khalidwe kwanu, kwa machimo osalapa a inu okhulupirira, kukhoza kuwupangitsa mpingo uwu kulephera moipa. Ndipo pa Tsiku la Chiweruzo inu mudzakayankhira gawo lirilonse la izo. “Oh,” inu mukuti, “tsopano, dikirani miniti, M’bale Branham.” Chabwino, chimenecho ndi Choonadi. Taganizani za izo!

⁵⁵ Yoswa, iye atatha kuwolokera mdzikolo, Mulungu anamupatsa iye lonjezo limene... Tangoganizani, kumenya nkondo yonseyo opanda kutaya munthu mmodzi, opanda ngakhale kukandika nkomwe, opanda ngakhale kukhala ndi namwino, kapena chithandizo choyambirira kapena bandeji. Amen. Mulungu anati, “Dzikolo ndi lanu, pitani mukamenyere.” Taganizani, za kumenya nkondo, ndipo opanda kukhala ndi a Red Cross nkomwe pafupi, palibe aliyense amene ati akavulale!

⁵⁶ Ndipo iwo anawapha a Amori ndi a Hitti, koma kunalibeko mmodzi amene anavulala pakati pa aliyense wa iwo mpaka tchimo litadzabwera mu msasa. Ndipo pamene Akani anadzatenga chovala cha wachi Babeloni uja ndi chikute cha golide chija, ndi kukazibisa izo pansu pa msasa wake, atatero tsiku lotsatira iwo anataya amuna sikisitini. Yoswa anati, “Imani! Imani! Dikirani miniti, pali chinachake chimene chalakwika! Chinachake chalakwika apa. Ife tiitanitsa kusala kwa masiku seveni. Mulungu anatipangira ife lonjezo, ‘Sipadzakhala chirichonse chiti chidzativulaze ife.’ Adani athu adzagwera pa mapazi athu. Ndipo pali chinachake chalakwika apa. Chinachake chalakwika penapake, chifukwa ife tiri ndi amuna sikisitini omwe afa agona apa. Iwo ndi abale achi Israeli, ndipo iwo afa.”

⁵⁷ Nchifukwa chiyani iwo anafa, munthu wosalakwa? Chifukwa munthu mmodzi anachoka pa mzere. Inu mukuwona chifukwa chimene izi zikuyenera kuphunzitsidwa? Mpingo uzifola, uzifola ndi Mawu a Mulungu, uzifola ndi Mulungu

ndipo uzifola ndi wina ndi mzake, kumayenda mwangwiro mowongoka, moganiza bwino, pamaso pa anthu onse, kumawopa Mulungu. Chifukwa munthu mmodzi ataba chovala, ndipo atachita chinachake chimene iye samayenera kuti achite, zinatenga moyo wa anthu sikisitini! Ine ndikuganiza anali sikisitini, mwinamwake ochulukirapo. Ine ndikukhulupirira anali amuna sikisitini amene anafa.

⁵⁸ Yoswa anaitanitsa, anati, “Pali chinachake chalakwa! Mulungu anapanga lonjezo, ndipo chinachake chalakwa.”

⁵⁹ Pamene ife tibweretsa odwala pamaso pathu, ndipo iwo nkulephera kuti achiritsidwe, ife timayenera kuti tiziitanitsa kusala kwaulemu, tiziitanitsa msonkhano. Chinachake chalakwa penapake. Mulungu anapanga lonjezo, Mulungu akuyenera kukakamira ku lonjezo limenelo, ndipo Iye adzachita izo.

⁶⁰ Ndipo iye anaitanitsa kusala. Ndipo iwo anadzapeza kuti, iwo anapanga maere. Ndipo Akani anavomereza izo. Ndipo iwo anamupha Akani, banja ndi onse, ndipo anawotcha maphulusa awo, ndipo analisisa ilo kumeneko ngati chikumbutso. Ndipo Yoswa anapitirira kudutsa mu nkhondoyo, kumatenga chirichonse, opanda kukandika kapena bala. Ndi zimenezotu.

⁶¹ Tsiku lina iye ankafuna kanthawi pang’ono, nthawi yowonjezera. Dzuwa linali likukalowa, amunawo samatha kumenya bwino bwino pa nthawi ya usiku. Yoswa, wankhondo wamkulu uja, wodzozedwa wa Mulungu, woikidwa pamalo mu dzikolo, monga Aefeso ku Mpingo watsopano, kutenga, analitenga, kulitenga dziko, kulilanda ilo. Iye ankafuna kanthawi, chotero iye anati, “Dzuwa, ima njii!” Ndipo ilo linaima njii kwa pafupifupi maora thwelofu, mpaka iye atalitenga dzikolo. Mukuona?

⁶² Tsopano Bukhu la Aefeso limatiika ife pamalo athu mwa Khristu, chimene iwo anali mu Dziko Loyera. Ife sitikuikidwa mu Dziko Loyera, koma mwa Mzimu Woyera! Tsopano tiyeni ife tingowerenga Mawu, tiwone mmene mpingo uliri wangwiro:

Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, . . .

⁶³ Oh, ine ndikuzikonda zimenezo! Mulungu anamupanga iye kukhala mtumwi. Panalibe ma eledara amene anadzaika manja pa iye, panalibe mabishopu amene anamutumiza iye kulikonse, koma Mulungu anamuitana iye ndipo anamupanga iye kukhala mtumwi.

Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, kwa oyera (iwo oyeretsedwawo) amene ali ku Efeso, ndi kwa okhulupirika mwa Yesu Khristu:

⁶⁴ Penyani mmene iye akuyankhulira izi. Izi si za kwa osakhulupirira. Izi ndi za kwa mpingo. Izo zikuitanidwira kwa

oitanidwa atuluke awo, oyeretsedwa ndi oitanidwa amene ali mwa Khristu Yesu.

⁶⁵ Tsopano, ngati inu mukufuna kuti mudziwe mmene ife timalowera mwa Khristu Yesu, ngati inu mungatsegule ku Akorinto Woyamba 12, iye amati, “Pakuti mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi.” Motani? Pobatizidwa motani? Mzimu Woyera. Osati mwa ubatizo wa mmadzi, inu anthu a Church of Christ, koma mwa chilembo chachikulu M-z-i-m-u, mwa Mzimu umodzi. Osati mwa kugwirana chanza kumodzi, mwa kalata imodzi, osati mwa kukonkha kumodzi. Koma, “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi,” cholowa chathu, Dziko limene Mulungu anatipatsa ife kuti tizikhalamo, Mzimu Woyera. Chimodzimodzi basi monga Iye anamperekerwa Kenani kwa Ayuda, Iye watipatsa ife Mzimu Woyera. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kukalowa mu Thupi limodzi.” Inu mukumvetsa zimenezo?

⁶⁶ Tsopano, iye akuyankhula kwa Akenani auzimu, Israeli, Israeli wauzimu amene watenga dziko. Oh, kodi sindinu okondwa kuti mwachoka ku gariki waku Igupto? Kodi sindinu okondwa kuti mwatuluka mchipululu? Ndipo, kumbukirani, iwo ankayenera kuti azidya manna, chakudya cha Angelo chochokera Kumwamba, mpaka iwo atawoloka kukalowa mdzikolo. Ndipo pamene iwo anadzawoloka kukalowa mdzikolo, manna anasiya kugwa. Iwo anali atakhwima kwathunthu nthawi imeneyo, ndipo iwo amadya chimanga chakale cha mdzikolo. Tsopano, tsopano pakuti sindinu makanda panonso, tsopano pakuti inu simukukhumbanso mkaka woyenera wa Uthenga, kuti inu simukusowa kuti muzichita kuleledwa, ndi kususitidwa, ndi kumachita kunyengereredwa kuti mubwere ku tchalitchi, tsopano pakuti ndinu Akhristu okhwima kwathunthu, ndinu okonzeka kudya chakudya cholimba tsopano. “Ndinu okonzeka kuti mubwere ku chinachake,” iye anatero. Ndinu okonzeka kuti mumvetse chinachake chimene chiri chakuya ndi chodula. Oh, ife tilowa mu zimenezo molunjika. Ndipo, oh, izo zakhala zobisidwa kuyambira pa maziko a dziko lapansi. Iye anati, “Tsopano pakuti inu mwabwera mu izi, ine ndikuyankhula izi kwa inu.” Osati kwa iwo amene angochoka kumene ku Igupto, osati kwa iwo amene akadali pa ulendo, koma kwa iwo amene ali mdziko lolonjezedwa, amene alandira lonjezo.

⁶⁷ Ndi angati amene analandira lonjezo la Mzimu Woyera? Oh, kodi sindinu okondwa kuti muli mdziko? Muli kuno tsopano, mukudya chimanga chakale, mukudya zinthu zolimba za Mulungu ndipo muli nako kumvetsa komveka. Anu—maganizo anu onse auzimu ndi osasokonezeka. Inu mukudziwa ndendende kuti Iye ndi ndani. Inu mukudziwa ndendende chimene Iye ali. Inu mukudziwa ndendende kumene inu mukupita. Inu

mukudziwa ndendende zonse za Izo. Inu mukudziwa mwa Amene inu mwamukhulupirira ndipo ndinu wokhutitsidwa kuti Iye ndi wokhoza kusunga chimene inu mwachipereka kwa Iye mu tsikuli. Oh, ndi ameneyotu, ameneyo ndi yemwe Paulo akuyankhulana naye tsopano. Mvetserani mwatcheru. Tsopano penyani.

...okhulupirika mwa Khristu Yesu:

⁶⁸ Tsopano, ndikufuna mpingo ubwereze zimenezo. Ife timalowa chotani mwa Khristu? Pojowina mpingo? Ayi. Poika dzina lathu pa bukhu? Ayi. Pobatizidwa mwakumiza? Ayi. Timalowa chotani mwa Khristu? Mwa Mzimu Woyera umodzi ife tonse timabatizidwa kukalowa mu lonjezo limodzi, Thupi, ndipo timakhala otenga nawo a zonse zimene ziri za mdzikolo. Ameni! Oh, ine—ine ndikuzikonda zimenezo. Ngati ine ndikanakhala kuti sindinasase mawu, ine ndikanafuula. Mai, pamene ine ndidzafike mu dziko ili, ilo ndi langa. Ine ndiri kwathu tsopano; ine ndiri mu Kenani. Ndine womvera kwa chirichonse chimene Mulungu akufuna kuti andigwiritseko ntchito. Ine ndikuyenda mmalo ojera, mwana wa Mfumu, yense wovekedwa mwinjiro ndipo wokonzeka. Ine ndatuluka ku Igupto, ndabwera kudutsa mdziko lolonjezedwa, ndapirira mayesero, ndadutsa ku Yordani ndipo ndafika ku lonjezo lodala ili. Oh, ine ndinazipeza motani izo? Mwa Mzimu umodzi. Mwanjira yomweyo imene Paulo anawupezera Iwo, unachita pa ine mwanjira yomweyo imene Iwo unachitira pa iye, mwanjira yomweyo imene Iwo unachitira pa inu. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa.” Osati kukonkhedwa, kukonkha pang’ono chabe kwa Iwo, kumverera bwino kwambiri; koma kumizidwa pansi! Zonse kupangitsidwa kuti zisambire pansi, mu Mzimu Woyera. Ndiro lonjezo.

⁶⁹ Aefeso wathu, Yoswa wathu, amene ali Mzimu Woyera, *Yoswa* amatanthauza “Yesu, Mpulumutsi.” Yoswa kutanthauza Mzimu Woyera kuimira izo mwauzimu monga izo zinali mu thupi, kuti Iye ndi Wankhondo wathu wamkulu. Iye ndi Mtsogoleri wathu wamkulu. Chimodzimodzi monga Mulungu anali ndi Yoswa, chomwechonso Mulungu (mwa Mzimu Woyera) akutiyendetsa ife. Ndipo pamene tchimo libwera mu msasa, Mzimu Woyera umafuna kuimikira, “Chalakhwika ndi chiyani mu mpingo uno? Chinachake chalakhwika.” Oh, inu simukuwona mmene ife takhalira ndi ana aamuna ambiri a Kish tsopano? A Saulo ochuluka akubwera kuchokera ku maseminare ndi masukulu a zaumulungu ndi kumapita kunja ndi kumakaphunzitsa zinthu zopotozedwa izi, monga Baibulo linanena kuti iwo akanadzachita. “Mowoneka, opanda Chikhulupiriro, kudzilekanitsa okha kwa inu, opanda chiyanjano ndi inu, ndi zina zotero, okhala nawo mawonekedwe aumulungu ndipo nkumakana mphamvu yake: kwa iwo chokaniko.” Iwo sakudziwa kumene iwo anachokera, iwo sangapereke chifukwa chirichonse.

⁷⁰ Ine ndikunena izi kuchokera kwa M'bale Booth Clibborn, mzanga wa ine, ngati pali chirichonse chimene chiri-... chapathengo chosalengedwa ndi umulungu, chirichonse mdziko, ndi mphongolo. Mphongolo ndi chotsikitsitsa cha zinthu zonse. Iye ndi a... iye—iye samadziwa chimene iye ali. Iye sangathe kudzibereka yekha nkomwe. Mphongolo sangakweranitsidwe ndi mphongolo imzake ndi kudzakhalanso mphongolo. Iye waltedwa. Iye samadziwa kumene abambo ake amachokerako, komanso samawadziwa amayi ake, pakuti iye ndi wamng'ono—bulu wamng'ono ndi kavalo wamba. Mulungu sanapange konse zimenezo. Musamaziike zoterozo pa Mulungu. Mulungu sanapange konse zimenezo. Mulungu anati, “Chirichonse chidzabala za mtundu wake.” Inde, bwana. Koma mphongolo ndi—a... bambo ake anali bulu ndipo mayi ake anali kavalo wamba, chotero iye samadziwa kuti iye ndi wandani. Iye—iye—iye ndi kavalo woyesetsa kuti akhale mphongolo, kapena mphongolo... kapena—kapena iye ndi kavalo woyesetsa kuti akhale bulu, bulu akuyesetsa kuti akhale kavalo. Iye samadziwa kuti iye ndi wakuti. Ndipo iye ndi chinthu chouma mutu chimene chiripo mdziko. Inu simungaike konse chidaliro chirichonse pa iye.

⁷¹ Ndipo umo ndi mmene anthu ambiri aliri mu mpingo. Iwo samadziwa kuti bambo wawo ndi ndani, iwo samadziwa kuti mayi wawo ndi ndani. Chinthu chokhacho chimene iwo amachidziwa, mwinamwake iwowo ndi a Presbateria, Methodist, Baptisti, kapena Pentekoste, kapena chinachake. Iwo samadziwa kumene iwo anachokera. Ndipo bulu wokalamba, inu mukhoza kumukuwira iye mmene inu mungafunire kumukuwa iye, ndipo iye amangoima pamenepo ndi kuimitsa makutu aakulu awo, ndi kumangoyang'ana. Iwe ukhoza kulalikirira kwa iwo utali wa usiku wonse, ndipo akamachokapo osadziwa konse kalikonse kuposa mmene amadziwira pamene amadzalowa. Tsopano, izo ndi kulondola basi. Ine sindikutanthauza kuti ndikhale wamwano, koma ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu Choonadi.

⁷² Koma pali chinthu chimodzi chimene iwo amakhoza kuchita, iwo ndi ogwira bwino ntchito. Oh, iwo amangogwira, kugwira, kugwira, kugwira. Zimenezo zimandiika ine mmalingaliro a gulu la Achiarminia ili amene nthawizonse amayesetsa kugwirira ntchito ulendo wawo wopita Kumwamba. Uko nkulondola, mphongolo. Oh, a Ladies Aid Society, ndi mgonero wa nkhuku, ngati malipiro, a mlaliki. “Ndipo tikhale ndi zovina izi, ndi zosangalala izi.” Iyo imangokhala ntchito, ntchito, ntchito, ntchito, ntchito, ntchito. Ndipo, iwo, kodi iwo akugwirira ntchito chiyani?

⁷³ Ukawafunsa iwo, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuyambira pamene inu munakhulupirira?”

⁷⁴ Iwo amaimitsa makutu awo, ndipo iwo samadziwa kuti iwo ndi akuti, “Kodi inu mukutanthauza chiyani? Ndikuti kumene kunachitika zonse *izi*? Inu mukutanthauza chiyani, Mzimu Woyera? Ine sindinamvepo chirichonse cha Iwo. Oh, iwe ukuyenera kukhala mtundu winawake wa otengeka.” Mwaona, iwo samadziwa kuti bambo anali ndani, kapena amayi anali ndani, aponso. Ndipo iwe umachita kuwamenya iwo pa chirichonse chimene iwe ukuchita, kumenya *apa* ndi kudzamenya *apo*, ndi kumenya *apa* ndi kudzamenya *apo*. Uko nkulondola, mphongolo yakale.

⁷⁵ Koma, ine ndikukuuzani inu, inu simumasowa kuchita zimenezo ndi kavalo wa mtundu weniweni. Mukangomukwapula iye kamodzi chikwapu, ndipo m’bale, iye wapita. Iye amadziwa chimene iye akuchita. Oh, zimakhala zabwino bwanji kukwera wa mtundu weniweniyo! Zimakhala zabwino bwanji kunena kuti, “Tiyeko, mnyamata.” Oh, mzanga, zingakhale bwino kuti ugwiritsitse, angachiponyere mmwamba chishalocho.

⁷⁶ Umo ndi mmene zimakhallira ndi Akhristu enieni. Aleluya! “Landirani inu Mzimu Woyera. Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu.” Amapita, basi mwamsanga monga mmene iwo angathere kupita ku madzi, iwo amapita. Iwo sangapume usana ndi usiku mpaka iwo atalandira Mzimu Woyera. Bwanji? Inu mukudziwa, Mkhristu amadziwa kuti Bambo ake anali ndani. Mwaona, zimatengera awiri kuti pakhale kubadwa. Uko nkulondola, bambo ndi mayi. Mphongolo siimadziwa kuti bambo anali ndani, kapena amayi anali ndani. Koma ife timadziwa kuti Bambo ndi Mayi anali Ndani, pakuti ife tinabadwa mwa Mawu olembedwa a Mulungu, tinatsimikiziridwa ndi Mzimu. Petro anatero, pa Tsiku la Pentekoste, “Ngati inu mulapa ndi kubatizidwa, mmodzi aliyense wa inu, mu Dzina la Yesu Khristu, ku chikhululukiro cha machimo anu, inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.”

⁷⁷ Ndipo, m’bale, Mkhristu weniweni wobadwa mwatsopano, (oh, mai) mzimu wake, mwamsanga iye akalandira Mawu, iye amalandira Mzimu Woyera. Mfunzeni iye chinachake nthawi imeneyo! Iye amadziwa pamene iye wayima. “Kodi inu mumakhulupirira mu machiritso Auzimu?”

“Ameni!”

“Kodi inu mumakhulupirira mu Kudza Kwachiwiri?”

“Ameni!”

⁷⁸ Ifunzeni mphongolo zimenezo. Chipembedzo cha mphongolo, “Uh, ine sindikudziwa. Dokotala Jones ananena nthawi ina . . .” Huh! Pamenepo, akumutsatira Saulo. Mukuona?

“Oh, iwo sakudziwa. Chabwino, ine ndikukuuzani inu, mpingo wanga siuli wotsimikiza za Izo.”

⁷⁹ Oh, m’bale, koma mwamuna wobadwa mwatsopano ndi mkazi amakhala otsimikiza basi za kudza kwa Ambuye Yesu, iwo amakhala otsimikiza basi kuti analandira Mzimu Woyera pakuti Mzimu Woyera ulipo woti uperekedwe.

⁸⁰ Tsopano, Yesu anati...Mkazi pa chitsime, “Ife timapembedza mu phiri ili, ndipo Ayuda amapembedza ku Yerusalemu.”

⁸¹ Iye anati, “Mkazi, mvera Mawu Anga! Ora likubwera, ndipo tsopano liripo, pamene Atate akufuna iwo amene azimupembedza Iye mu Mzimu ndi Choonadi.”

⁸² “Mawu Anu ali Choonadi.” Ndipo munthu aliyense amene adzawerenga Baibulo ndi kukhulupirira Mawu aliwonse amene Baibulo likunena, ndi kutsatira malangizo Ake, ndi kulandira Mzimu Woyera womwewo umene iwo analandira, mwanjira yomweyo imene iwo analandilira Iwo, zotsatira zomwezo zimene iwo analandilira Iwo, mphamvu yomweyo imene iwo anaipeza pamene analandira Iwo, iye amadziwa yemwe Bambo wake ndi Amayi anali. Iye amadziwa kuti iye anasambitsidwa Mmagazi a Yesu Khristu, anabadwa mwa Mzimu, anadzazidwa ndi kudzodza kwa Mulungu. Iye amadziwa pamene iye akuima. Ndithudi! Iye ali mu Kenani. Iye amadziwa kumene iye anachokera. Umo ndi mmene zimakhalira ndi Mkristu weniweni. Mukamufunsa iye, “Kodi iwe unalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?”

“Ameni, M’bale!”

⁸³ Nditaima tsiku lina pafupi ndi woyera wakale, usinkhu wa zaka nainte-thuu, akuyankhulana ndi m’busa wake wa usinkhu wa zaka eyite, ine ndinati, “Agogo aakazi?”

Wowala basi monga mmene iye akanakhallira, iye anati, “Inde, mwana wanga.”

⁸⁴ Ine ndinati, “Zatenga nthawi yaitali bwanji kuyambira pamene munalandira Mzimu Woyera?”

Iye ndinati, “Ulemelero kwa Mulungu! Pafupifupi zaka sikisite zapitazo ine ndinalandira Iwo.”

⁸⁵ Tsopano, ngati iye akanakhala mphongolo, iye akanati, “Tsopano, dikira miniti, ine ndinatsimikiziridwa ndipo ndinakonkhedwa pamene ine ndinali...Chabwino, ndithudi, ndipo iwo anandilowetsa ine mu tchalitchi ndipo ndinampatsira kalata yanga *wakuti*.” Oh, chifundo ine! Iwo samadziwa nkomwe kuti iwo ndi andani.

⁸⁶ Koma iye amadziwa kumene ufulu woyamba kubadwa kwake umachokera. Iye anali pamenepo pamene izo zinkachitika. Iye anabadwa mwa madzi ndi Mzimu. Iye

ankadziwa, ndipo madzi kudzera mu kusambitsidwa kwa madzi mwa Mawu, umatenga Mawu.

⁸⁷ Tsopano penyani momwe akuyankhulira izi, “Kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu.” Paulo, tsopano, kumbukirani. . . Ine ndikutenga nthawi yaitali, koma ine sindimaliza mutu uwu. Koma ine ndifulumira. . . Kodi inu mukuzikonda izi? Oh, Iwo akuti uza ife pamene ife tiri, koma ife sitingathe kuchita izo mu usiku umodzi wokha. Ife tikusowekera mwezi umodzi kapena iwiri ya izi, usiku uliwonse, basi kumangopita kudutsa Iwo, Mawu ndi Mawu. Kubwerera mmbuyo ndi kukazisakatula izo kuchokera mu mbiriyakale ndi kudzaziya izo, Mawu ndi Mawu, ndi kudzakuwonetsani inu kuti Icho ndi Choonadi. Tsopano mundilole ine ndiwerenge ndime imeneyo mwachangu kenanso.

Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu (osati chifuniro cha munthu), kwa oyera amene ali mu Efeso, ndi (mlumikizi) kwa okhulupirika mwa Khristu Yesu:

⁸⁸ Zikutanthauza, “Iwo ayitanidwa atuluke, alekanitsidwa, ndipo tsopano abatizidwa mwa Mzimu Woyera, ndipo ali mwa Khristu Yesu. Ine ndikulemba kalata iyi kwa inu, okondedwa anga.” Oh! Ine ndikuganiza za Paulo kumeneko ali ndi iwo tsopano, oh, ndine wokondwa bwanji! Mtumwi wakale wamng’ono uja mutu wake unadulidwa kumusi uko. Ine ndinaima pafupi ndi malo amene iwo anamudula mutu wake. Koma, oh, mutu wake uli pa thupi la tsopano ilo, ndipo sungadulidwenso nkomwe. Ndipo iye waima pamene ndi iwo miniti yomwe ino, mtumwi yemweyo amene analemba Izi. Ndipo anati, “Kwa inu amene muli mwa Khristu Yesu! Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi ili.” Tsopano penyani.

Chisomo chikhale kwa inu, ndi mtendere, kuchokera kwa Mulungu Atate athu, ndi. . . Ambuye Yesu Khristu.

Wodala ndi Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, amene watidalitsa ife ndi zonse. . .

Oh, iwe ukumva zimenezo, Charlie?

. . . amene watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu. . .

⁸⁹ Osati kungoti ena kwa atumwi, ndi ena kwa *ichi*, koma Iye watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu. Mzimu Woyera womwewo umene unadzagwa pa Tsiku la Pentekoste ndi Mzimu Woyera womwewo pano usikuuno. Mzimu Woyera umene unamupangitsa Maria kufuula ndi kuyankhula ndi malirime, ndi kukhala ndi nthawi yopambana ndi kukondwerera, ndi zinthu zimene iye anachita, ndi Mzimu Woyera womwewo pano usikuuno. Mzimu Woyera womwe uja umene unamulola Paulo pa ngalawa yakale ija, pamene zinkawoneka ngati iyo

yadzaza madzi ndipo ikumira, ndipo masiku fortini ndi mausiku, kopanda mwezi kapena nyenyezi. Iye anayang'ana kunja uko ndipo funde lirilonse linali ndi mdierekezi pa ilo, akuyang'ana, ndi kumanyezimiritsa mano ake, ndipo anati, "Ine ndikumiza iwe, mnyamata wakale, tsopano. Ine ndakupeza iwe tsopano."

⁹⁰ Ndipo pamene Paulo anatsikira mmusi kuti akakhale ndi kapemphero kakang'ono, pamenepo panadzaima Mngelo, anati, "Usawope, Paulo. Ngalawa yakale iyi ikaphwasukira pa chisumbu chinachake. Kazipita ndipo ukadye chakudya chamadzulo chako, izo zikhala bwino tsopano."

⁹¹ Apa iye akubwera ali ndi unyolo umenewo pa mikono yake yaing'ono yokalamba, akukwakwaza iwo pa mapazi ake, ndipo anati, "Khalani olimba mtima, amuna, pakuti Mulungu, Mngelo wa Mulungu, amene ine ndiri wantchito wake, anaima pafupi ndi ine ndipo anati, "Paulo, usawope ayi." Mzimu Woyera womwewo uli pano usikuuno, Mzimu wa Mulungu womwewo, ukutumikira kwa ife madalitso auzimu omwewo.

... anatalitsa ife ndi madalitso onse auzimu mmalo a mmwambamwamba...

⁹² Oh, tiyeni tiime miniti inanso apa. "Mmalo a Mmwambamwamba." Tsopano, basi osati kungokhala kulikonseko, koma mmalo a Mmwambamwamba. Ife tasonkhana "Mmwambamwamba," zimatanthauza kuti malo a wokhulupirira. Kuti, ngati ine ndapemphera, inu mwapemphera, kapena mpingo wapemphera, ndipo ife nkukhala okonzekera Uthenga, ndipo tadzisonkhanitsa tokha pamodzi ngati oyera, oyitanidwa atuluke, obatizidwa ndi Mzimu Woyera, odzazidwa ndi madalitso a Mulungu, oyitanidwa, osankhidwa, kukhala pamodzi mmalo a Mmwambamwamba tsopano, ife ndi a Mmwambamwamba mu masolo athu. Mizimu yathu yatibweretsa ife kudzalowa mu chikhalidwe cha Mmwambamwamba. Oh, m'bale! Ndi zimenezotu, chikhalidwe cha Mmwambamwamba! Oh, chingachitike ndi chiyani usikuuno, chingachitike ndi chiyani usikuuno ngati ife tikanati tikukhala pano mu chikhalidwe cha Mmwambamwamba, ndipo Mzimu Woyera ukuyendayenda pa mtima uliwonse umene wakonzedwanso ndipo wasanduka cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu? Machimo onse atakhala pansu pa Magazi, mu kupembedza kwangwiro, manja athu atakwezedwa mmwamba kwa Mulungu ndipo mitima yathu itakwezedwa, titakhala mmalo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu, tikupembedza limodzi mmalo a Mmwambamwamba.

⁹³ Kodi inu munayamba mwakhalapo mwa amodzi? Oh, ine ndinakhalapo mpaka ine kumalira ndi chimwemwe ndikuti, "Mulungu, musandilole konse kuti ndichoke pano." Basi kungokhala mmalo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu!

⁹⁴ Kutidalitsa ife ndi chiyani? Machiritso Auzimu, kudzodzedweratu, vumbulutso, masomphenya, mphamvu, malirime, kutanthauzira, nzeru, chidziwitso, madalitso onse a Mmwambamwamba, ndi chimwemwe chosaneneka ndi wodzaza Ulemelero, mtima uliwonse utadzazidwa ndi Mzimu, kumayenda limodzi, kumakhala limodzi mmalo a Mmwambamwamba, opanda lingaliro loipa lililonse pakati pathu, opanda ndudu imodzi yosutidwa, opanda chovala chachifupi chimodzi, opanda *ichi*, *icho* kapena *chinacho*, opanda lingaliro loipa limodzi, opanda winawake wokhala ndi mangawa pa wina ndi mzake, aliyense kumayankhula mwa chikondi ndi mwachiyanjano, aliyense ndi mtima umodzi pa malo amodzi, “kenako mwadzidzidzi pamenepo panadzabwera kuchokera Kumwamba nkokomo ngati mphepo yankuntho.” Ndi zimenezotu, “Watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu.”

⁹⁵ Kenako Mzimu Woyera ukhoza kugwera pa winawake, ndikuti, “PAKUTI ATERO AMBUYE. Pita ku malo ena ake ndipo ukachite chinthu chinachake.” Muwone icho chikuchitika basi monga *chomwecho*. [M’bale Branham akukhwatchitsa chala chake—Mkonzi] Mukuona? “PAKUTI ATERO AMBUYE. Ukachite chinthu chinachake pa malo ena ake.” Muchiwone icho chikuchitika basi monga *choncho*. [M’bale Branham akukhwatchitsa chala chake]

⁹⁶ “Watidalitsa ife limodzi mu madalitso onse a Mmwambamwamba mmalo a Mmwambamwamba.” Penyani!

Monga momwe iye watisankhira ife . . .

⁹⁷ Kodi ife tinamusankha Iye, kapena Iye anatisankha ife? Iye anatisankha ife. Liti? Usiku umene ife tinamulandira Iye? Anatisankha!

Monga momwe iye anatisankhira ife mwa iye maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, kuti ife tidzakhale oyera . . . opanda chilema pamaso pa iye mwa . . . (zipembedzo?) . . . mu chikondi:

⁹⁸ Ndi liti limene Mulungu anatisankha ife? Ndi liti limene Mulungu anakusankhani inu amene muli ndi Mzimu Woyera? Ndi liti limene Iye anakusankhani inu? Maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Mwa kudzodzeratu Kwake, Iye anakuwoneranitu inu ndipo anadziwa kuti inu mukanadzamukonda Iye. Ndipo asanakhalepo maziko a dziko lapansi, Iye anakusankhani inu, ndipo anamutumiza Yesu kuti Iye adzakhale chitetezero cha machimo anu, kuti adzakuitanireni inu ku chiyanjanitso, kwa Iyemwini, ku chikondi. Oh, ndikanakonda tikanakhala ndi nthawi ya maminiti angapo owonjezera.

⁹⁹ Ndiloleni ine, ife tisanapite patsogolo paliponse, ndibwerere mmbuyo, Genesis 1:26. Ine ndidzazitenga izo Lachitatu. Pamene Mulungu anamupanga munthu . . . Iye asanamupange munthu,

Iye ankadzitcha Iyemwini “El,” E-l, El; E-l-h, “Elah,” “Elohim.” Liwulo limatanthauza, mu Chihebri, “wokhalapo-yekha,” zonse mwa Iyemwini. Palibe chimene chinakhalapo Iye asanakhalepo, Iye anali wokhalapo yekha amene anakhalapo, Uyo wokhalapo-yekha! El, Elah, Elohim, amatanthauza “wokwanira mu zonse, wamphamvu-zonse, Wamphamvuzonse, Uyo wokhalapo-yekha.” Oh!

¹⁰⁰ Koma mu Genesis 2, pamene Iye anamupanga munthu, Iye anati, “Ine ndine,” Y-a-h-u, J-u-v-u-h, *Yahweh*, “Yehova.” Kodi izo zimatanthauza chiyani? “Ine ndi Uyo wokhalapo yekhayo Amene ndinalenga chinachake kuchokera mwa Inemwini, kuti chidzakhale mwana wa Ine, kapena wongoyembekezera, kapena wamng’ono, wachichepere wa Ine.” Ulemelero! Bwanji? Iye anamupatsa munthu... *Yehova* amatanthauza kuti “Iye anampatsa munthu kuti adzakhale mulungu wamng’ono.” Chifukwa Iye ndi Mulungu Atate, ndipo Iye anamupanga munthu kukhala mulungu wamng’ono, chotero Iye si wokhalapo yekhanso, Iye akukhala ndi banja Lake. Elah, Elah, Elohim. Tsopano, tsopano Iye ndi Yehova. *Yehova*, kutanthauza, “Mmodzi Amene akukhala ndi banja Lake.” Tsopano, Mulungu anamupanga munthu kuti adzakhale wolamulira pa dziko lapansi lonse, iye anali ndi ulamuliro. Ndipo dziko lapansi linali ulamuliro wa munthu. Kodi limenelo ndi Lemba? Ndiye ngati umenewo uli ufumu wake, iye anali mulungu pa dziko lapansi. Iye amatha kuyankhula, ndipo zimakhala chomwecho. Iye amatha kuyankhula *ichi*, ndipo chimachitika chomwecho. Oh! Ndi Ameneyotu, Mulungu, Yehova, Mmodzi Amene anakhalapo mu kukhalapo yekha, koma tsopano akukhala ndi banja Lake, ndipo ndi ana Ake limodzi ndi Iye. Ndi zimenezotu.

¹⁰¹ Tsopano, mukawerenge zimenezo. Ife tidzalowa mu zimenezo Lachitatu usiku, pamene ife tidzakhale ndi nthawi yambiri. Ife tangotsala ndi maminiti fifitini ena owonjezera ndipo ife ti... Ine ndimaganza kuti ndifika pamalo ena ake apa, koma ife sititero, kufika pamene ife tasindikizidwa ndi Mzimu Woyera wa lonjezo. Chabwino.

¹⁰² Tsopano, kodi ife tinaitanidwa liti kuti tidzakhale antchito a Mulungu? Ndi liti limene Orman Neville anaitanidwa kuti adzakhale wantchito wa Mulungu? Oh, mai! Izi zimandipangitsa ine kudzandima. Ine ndikuuzani inu, tiyeni titenge Malemba ena. Ine ndikufuna inu mupeze Petro Woyamba 1:20. Ndipo, Pat, upeze Chivumbulutso 17:8. Ndipo ine ndipeza Chivumbulutso 13. Tsopano ife tikufuna kuti timvetsere apa, inu mukufuna kuti mudziwe kuti ndi liti limene Mulungu anakuitanani inu kuti mudzakhale Mkhristu. Oh, ine ndimazikonda izi. Izi, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Chabwino, M’bale Neville, inu mwapeza Petro Woyamba 1:20. [M’bale Neville akuti, “1:20.”—Mkonzi] Chabwino, muwerenge 1:19 ndi

1:20. Mvetserani kwa izi. [“1:19 ndi 20.”] Inde. [M’bale Neville akuwerenga Petro Woyamba 1:19-20]

Koma ndi magazi ofunika a Khristu, monga a mwanawankhosa wopanda chirema ndi wopanda banga:

Amene ndithudi anadzodzedweratu asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi, koma anawonetseredwa mu nthawi zotsiriza izi kwa inu.

¹⁰³ Ndi liti limene Iye anadzodzedweratu? Maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. M’bale Pat, ndiwerengereni ine Chivumbulutso 17:8. [M’bale Pat akuwerenga Chivumbulutso 17:8—Mkonzi]

Chirombo chimene iwe unachiwona chinalipo, ndipo palibepo; ndipo chidzakwera kutuluka kuchokera mu dzenje lopanda malire, ndi kudzalowa ku chitayiko: ndipo iwo okhala padziko lapansi adzadabwa, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo chikhazikitsireni cha maziko a dziko lapansi, pamene iwo adzawona chirombo chimene chinalipo, ndipo palibepo, ndipo komabe chiripo.

¹⁰⁴ Nndani ati adzanyengedwe? Nndani ati adzanyengedwe ndi munthu wachipembedzo uyu monga anachitira Sauli? Izo zinali zothyathyalika kwambiri chabe ndi zangwiro kwambiri mpaka izo zikanadzanyenga chiyani? Kumene Wo-... [Osonkhana akuti, “Wosankhidwa.”—Mkonzi] kukanakhala... [“kotheka.”] kukanakhala kotheka. Chabwino, Chivumbulutso 13:8, ndiloleni ine ndikuwerengereni inu:

Ndipo onse amene akukhala pa dziko lapansi adza... onse amene akukhala pa dziko lapansi adzamupembedza iye, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo wa Mwanawankhosa wophedwa asanakhazikitsidwe maziko a dziko lapansi.

¹⁰⁵ Maina athu anaikidwa liti mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa? Pamene Mwanawankhosa anaphedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Pamene Mulungu anali Yehova, El, Elah, Elohim, wokhalapo Yekhayo. Monga ngati Diamondi imodzi yaikulu, ndipo Iye sakanakhala chinachakenso, koma mkati mwa Diamondi iyi zikhumbo Zake zinali Mpulumutsi. Mu zikhumbo izi, mkati mwa Iye, munali Mchiritsi. Chabwino, panalibepo kanthu koti akapulumutse ndipo panalibe choti achichiritse, koma zikhumbo Zake zinabereka izo. Chotero, ndiye maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, pamene Iye ankadziwa, kuwonetsera kwakukuru apa kwa Iye, kuti Iye akanadzakhala Mpulumutsi, kuti Iye akanadzabwera ndi kudzasandulika thupi ndi kudzakhala pakati pathu, ndipo Iye ankadziwa kuti ndi mikwingwirima Yake ife tikanadzachiritsidwa, Iye anapha

Mwanawankhosa pa Bukhu Lake maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ndipo analemba dzina lanu pa Bukhu limenelo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Oh!

¹⁰⁶ Mvetserani kwa Ichi! Kukonzedweratu kumayang'ana mmbuyo ku kudzodzedweratu, ine ndikutanthauza kusankhidwa. Kusankhidwa kumayang'ana mmbuyo ku kudzodzedweratu, ndipo kukonzedweratu kumayang'ana kokafikira. Musaiwale zimenezo, kuti kusankhidwa kumayang'ana mmbuyo apa, ndi izi apa, "Ine ndinali chisoso. Ine ndinabadwa mu tchimo, ndinaleredwa mu kusaeruzika, ndinabwera ku dziko lapansi ndikuyankhula mabodza, ndinabadwa pakati pa ochimwa. Abambo ndi amayi ndi banja langa lonse, ochimwa. Ine ndinali chisoso. Koma, mwadzidzidzi, ine ndinadzakhala njere ya tirigu. Izo zinachitika motani?" Izo, ndi chiyani chimenecho? Kusankhidwa. Mulungu, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, anasankha kuti chisoso chidzakhala njere ya tirigu. "Tsopano ine ndikudziwa ndine njere ya tirigu, chifukwa ine ndinapulumutsidwa. Ine ndimachita motani izo?" Ndimayang'ana mmbuyo ndipo ndimawona kuti Iye anakonzeratu izo, kalekale. Mwa kudzodzedweratu Iye anawona kuti ine ndikanadzamukonda Iye, chotero Iye anakonza chitetezero kudzera mwa Mwana Wake Yemwe, kuti kudzera mwa Iye ine ndidzathe kuchoka ku chisoso kupita kudzakhala njere ya tirigu. "Tsopano, kodi ine ndiri pati tsopano?" Ndine wopulumutsidwa, ine ndikuyenda mu chisomo cha Mulungu. "Kodi kukonzedweratu kumayang'ana chiyani?" Kokafikira. "Kodi Iye adzanditengera ine kuti, ndipo kodi ine ndikupita kuti?" Ameni. Izo zakufikanipo inu. Ndi zimenezotu.

¹⁰⁷ Tsopano tiyeni tiwerenge mopitirira patsogolo pang'ono, ndipo kenako ife tiyenera titseke posakhalitsapa.

Monga mmene iye . . . anatisankha ife mwa iye maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, kuti ife tidzakhale ojera . . . opanda chilema pamaso pake mu chikondi:

Atatha kutikonzeratu ife ku kukhazikitsidwa, kukonzedweratu ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu kwa iyemwini, mogwirizana ndi kufuna kwabwino kwa chifuniro chake,

¹⁰⁸ Kodi Iye anachita chiyani? Iye, mwa kudzodzedweratu, anatiwoneratu ife, akudziwa kuti Iye anali Mpulumutsi, wokhalapo-yekha. Kunalibeko Angelo, kunalibe kalikonse; kunangokhala Mulungu, Elah, Elohim, Iye wokhalapo-yekhayo, kunalibe kalikonse koma Iye yekha. Koma mwa Iye munali Mpulumutsi. Chabwino, kodi Iye adzapulumutsa chiyani, kunalibeko kanthu kalikonse kamene kanataika? Podziwa zimenezo, ndiye Iye anadziwa kuti chikhumbo chachikulu ichi mwa Iye chikanadzatulutsa chinachake kutali uko chimene

Iye akanadzachipulumutsa. Kenako pamene icho chinachita chimenecho, mwa kudzodzedweratu Iye anayang'ana pansi ndipo Iye anamuwona aliyense amene akanadzavomereza Iwo. Ndiyeno pochita zimenezo, Iye anati, “Kuti ndipulumutse icho, njira yokhayo imene Ine ndingachitire izo, ikhala kutsika pansi Inemwini ndi kudzasanduka thupi ndi kukatenga tchimo la munthu pa Iye, ndi kumufera iye, kuti Ine ndidzakhale Mmodzi amene azidzapembedzedwa,” chifukwa Iye ndi Mulungu, chinthu chopembedzedwa.

¹⁰⁹ Kenako Iye anadzatsika pansi ndipo anadzadzitengera pa Iyemwini. Ndipo pamene Iye anachita zimenezo, Iye anachita zimenezo kuti Iye adzakupulumutseni inu amene mukufuna kupulumutsidwa. Kodi inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza? Mwa kudzodzedweratu, Mulungu wopandamalire, Amene ankadziwa zinthu zonse, anamuwona Mwanawankhosa, ndipo Iye anamupha Mwanawankhosayo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ndipo Iye anaika dzina lanu mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ndipo Iye anawona chinyengo cha Satana, chimene iye akanati adzachite. Chotero Iye anaika dzina lanu mmenemo. Ndipo Iye ananena kuti wotsutsakhristu adzakhala wachipembedzo kwambiri, wabwino kwambiri, munthu wabwino chomwecho, munthu wanzeru chomwecho, munthu wachipembedzo chomwecho, mwakuti iye akanadzanyenga Osankhidwa kumene ngati kukanakhala kotheke. Koma izo ndi zosatheka, chifukwa maina awo anadzodzedweratu maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Mwa kusankha Iye anawasankha iwo, ndipo mwa kukonzedweratu iwo amadziwa kumene iwo akupita. Ndi zimenezotu.

¹¹⁰ Tsopano, nndani angakaikire zimenezo? Izo ndi zimene Paulo amanena. Amenewo ndi Malemba a Paulo. Zimenezo ndi zolembe za Paulo. Izo ndi zimene ankawuphunzitsa mpingo wake. Mpingo, unaikidwa pamalo, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Pamene Mulungu, mu ululu Wake wakubala, anali kubala, ankakubweretsani inu, akudziwa zimene inu mukanadzachita, Iye anakuikani inu pamalo anu mu Thupi Lake Lomwe, kuti mudzakhale mkazi wapanyumba, kuti mudzakhale mlimi, kuti mudzakhale mlaliki, kuti mudzakhale mneneri, kuti mudzakhale *ichi* kapena *icho*. Iye anakuikani inu pa malo anu. Kenako pamene ife tinabwera kuchokera ku maiko a gariki ku Igupto, kudzera mu kuyeretsedwa, ndipo nkubatizidwa kukalowa mu dziko lolonjezedwa... Pakuti, lonjezo la Mulungu ndi Mzimu Woyera. Aefeso 4:30 amati, “Musawukhumudwitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiwombolo.” Kenako Mulungu, atatha kuwukonzedweratu mpingo, Iye anati, “Ndipo anthu onse, adzakhhalapo mamillioni kuchulukitsa mamillioni amene ati azidzayenda mwachipembedzo ndipo

adzanyengedwa.” Okhawo amene sadzanyengedwa adzakhala iwo amene awolokera mu dziko lolonjezedwa, amene maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe anali maina awo ataikidwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, ndipo adzalowa mdziko lolonjezedwa, ndipo akusangalala nalo ilo.

¹¹¹ Anthu ambiri amawopa kuti achita mowonjeza. Anthu ambiri amawopa Mzimu Woyera ukupangitsani inu kuchita chinachake chimene inu—inu mudzachite nacho manyazi kwa anthu. Anthu ambiri amawopa kuti alira, ndipo wokonedwa wawo awawona iwo akulira, kapena amayi, kapena woyandikana naye wanu, kapena abwana anu akuwonani inu.

¹¹² Mundilole ine ndikuuzeni inu za munthu nthawi ina, ndisanatseke. Panali munthu dzina lake Davide, ndipo pamene likasa la Mulungu linali liri ku dziko la Afilisiti, ndipo Ilo limabwera, likukokedwa ndi likasa, ng’ombe yokalamba imawakoka iwo, pamene Davide anawona likasa limenelo kuti likubwera, iye anali atavala mkanjo waung’ono pa iye, iye anathamangira kumeneko, anamenyetsa mapazi ake m’mwamba, ndipo analumphalumpha, ndipo anakuba ndi kulumphu, ndipo anavina ndi kulumphu ndipo anavina. Ndipo, iye, ali mfumu ya Israeli! Ndipo mkazi wake anadzayang’ana kudzera pa zenera ndipo anamuwona iye akuchita mwachilendo kwambiri, iye anamunyoza iye. Bwanji, iye ayenera kuti ananena kuti, “Chidempete! Tamuwonani iye uko, momwe iye akuchitira, mmene akuponyera mapazi ake m’mwamba, ndi kumalumphalumpha pamenepo ndi kumachita monga chomwecho. Bwanji, ayenera kuti wapenga!” Ndipo usiku umenewo pamene iye anadzalowa, iye anati, molankhula chonchi, “Bwanji, iwe wandichititsa ine manyazi. Bwanji, iwe, wokhala mfumu, mwamuna wanga, kunja kuja kumachita chonchija, kumachita chonchija!”

¹¹³ Davide anati, “Mawa ndidzachita bwinoko kuposa pamene paja. Inde, bwana!” Iye anati, “Kodi iwe sukudziwa kuti ine ndimavinira Ambuye?” Iye anali atawoloka! Iye anali ali mu dziko la lonjezo. Iye anali atataya za kudzimva-yekha zonsezo ndi matope a mdziko. Iye anali wokondwa kwambiri atadziwa kuti likasa linali kubwera mu mzinda wake womwe.

¹¹⁴ Ndipo, oh, ndikukuuzani inu, anthu ena amawopa kuti alandire Mzimu Woyera, amawopa kuti ayamba kuyankhula ndi malirime. Iwo amawopa kuti winawake akhoza kunena kuti, “Tsopano, iye ndi mmodzi wa anthu a zamalirime aja.” Iwo amawopa kuti abwere ku tchalitchi ndi kudzabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa chakuti iwo akuchita nalo manyazi Ilo. Uh! Oh!

¹¹⁵ Winawake akunena kuti ine ndikuyenera kuti ndikawachotseko matepi anga, chifukwa chakuti ndinali

nditalalikira za kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ine sindikukawachotsako iwo. Ine ndikupanga ochuluka! Uko nkulondola, kuti, ndikupanga ochuluka! Iwo ndi Baibulo. Ngati iwo sakuzikonda zimene ife tinachita dzulo, mungopenyetsetsa zomwe titi tipange mawa! Ndicho chinthu choti tizichita, mwaona, kumangoyendabe chitsogolo. Palibepo kuti iwo asiyika, chifukwa iwo ndi Ambuye. Iwo ndi Mulungu.

¹¹⁶ Inu mukudziwa chimene Mulungu anachita? Mulungu anayang'ana pansi kuchokera Kumwamba, Iye anati, "Davide, ndiwe mwamuna wa pa mtima Panga Pomwe." Davide samachita manyazi. Iye anali wantchito wa Ambuye. Iye ankawakonda Ambuye. Ndipo iye anali wokondwa kwambiri, anasangalala kwambiri, kufikira kuti sanaganizire za ulemerero wa umunthu.

¹¹⁷ Inu mukuona, monga ine ndinanenera mu ulaliki wanga m'mawa uja, ife timachita mantha kwambiri, mpaka, kuti timafuna Saulo kuti atiphunzitse ife, ife timafuna ka Saulo kochokera ku seminare inayake kuti kazitiphunzitsa ife momwe tikuyenera kuchitira chipembedzo chathu ndi momwe ife tikusteryenera tizichitira izi. Zimenezo ndi tsidya linalo la Yordani. Tsidya lino, Mzimu Woyera ukutsogolera. Kuno inu mumakhala kuti mwachokamo mmatope amenewo. Kuno inu simusamala zimene iwo akuganiza. Kuno inu mwafa, ndipo moyo wanu wabisidwa mwa Khristu kudzera... ndipo wasindikizidwa ndi Mzimu Woyera. Inu simusamala. Inu mukukhala mu Kenani. Inu mukhoza kudya chimanga chabwino. Ndinu cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu. Inu mukupita ku dziko lonjonzedwa.

¹¹⁸ Ine ndikukumbukira nditaima uko, M'bale Collins, zaka zina sarte zapitazo, pamene tchalichi ichi chinali chisanamangidwe. Zinali msonkhano waung'ono wa msasa ndinakhala apa pa ngodya, msonkhano wanga woyambirira. Ine ndinkalalikira Uthenga womwewu uwu, chinthu chomwechi, chuma chosafufuzika cha Khristu: ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu Khristu, kukhulupirira Mawu aliwonse kukhala Choonadi, ubatizo wa Mzimu Woyera, machiritso Auzimu, mphamvu za Mulungu, chimodzimodzi basi monga momwe ine ndikuulalikirira Iwo tsofano, sindinachokeko nkomwe inchi imodzi kwa chirichonse cha Iwo. Mulungu waululula zochuluka za Iwo kwa ine, chotero, pamene Iye akuwulula Iwo, ine ndimangopitiriza kumawubweretsapo Iwo. Iye sachotsapo nkomwe zimene zakhala ziripo, Iye amangokhala akupitiriza kumawonjezera zochuluka pa Iwo.

¹¹⁹ Ine ndinaima kumusi uko pamene pafupifupi anthu faifi handiredi anaima pa gombe, akuimba, "Ndaima pa gombe la nkuntho la Yordani, ndipo ndikuyang'anitsitsa, ndikupita ku Kenani dziko lokoma ndi lokondwa, kumene kuli chuma changa. Ndikadzafika ku malo athanziwo ndi kukadalitsika kwa

nthawizonse, ndikadzafikako ndi kudzakhala ya Atate anga . . . ndi kudzapuma kwanthawizonse?” Pamene iwo anayamba kuimba imeneyo, ine ndinali ndikumutengera mnyamata kukalowa naye mu mtsinje kuti ndikumubatize iye uko mu Dzina la Ambuye Yesu. Ine ndinati, “Atate a Kumwamba, pamene ine ndikumubweretsa mnyamata uyu kwa Inu pa kuvomereza kwake. . .” Ndiri mnyamata chabe, inemwini, ndiri nazo zithunzi za izo kunyumba. Ine ndinati, “Pamene ndikumubatiza iye ndi madzi, Ambuye, pa kuvomereza kwake, mu Dzina la Yesu Khristu Mwana wa Mulungu, Inu mumudzaze iye ndi Mzimu Woyera.” Ndipo pafupifupi nthawi imeneyo Chinachake chinayamba kuzungulira, ndipo apa Icho chimabwera chikuzungulira kumatsikira pansi, Nyenyezi Yowala ya M’wawa inadzaima pamene. Pamene panadzaima Kuwala kuja kumene inu mumakuwona apo pa chithunzi. Pamene Iko kunadzaima.

¹²⁰ Icho chinapita kuzungulira dziko lonse, mpaka uko ku Canada ndi kozungulira. Iwo anati, “Kuwala kodabwitsa kwawonekera pa mtumiki wamba wa Baptisti pamene iye amatiza.”

¹²¹ Masiku pang’ono apitawo, pamene Dokotala Lamsa anabwera kwa ine, ndipo samadziwa kalikonse ka izo, ndipo anandibweretsa ine chithunzi, chimene m’bale ali nacho icho uko tsopano. Kodi muli nacho chithunzi chija? Kodi Baibulo uli nalo, chiri mmenemo, chiri mu bukhu lako? Chabwino. Pamene panali chithunzi cha chizindikiro chakale cha amakedzana cha Chihebri cha Mulungu, ndendende basi chijachi chimene chinalipo m’masiku a Yobu, Baibulo lisanalembedwe nkomwe. Mulungu ali mu zikhumbo zitatu Zake, osati milungu itatu. Mulungu m’modzi mu zikhumbo zitatu: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, maudindo atatu amene Mulungu anagwiriramo ntchito. Osati milungu itatu, zikhumbo zitatu! Ndipo Icho chinali pamene. Pamene munthu wamkulu uja, Dokotala Lamsa, kumasulira kwa Baibulo la Lamsa, pamene iye ananena m’wawa umenewo. . . Pamene ine ndinamuza iye zimenezo, ine ndinati—ine ndinati, “Chizindikiro chimenecho ndi chiyani?”

¹²² Iye anati, “Chimenecho ndi chizindikiro chamakedzana cha Mulungu, mu Chihebri. Mulungu, Mulungu mmodzi mu zikhumbo zitatu.”

Ine ndinati, “Monga ngati Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera?”

¹²³ Iye anaimikira, ndipo anakhazika kapu yake ya khofi pansi, iye anandiyang’ana ine. Gene, ndikukhulupirira iwe unali pamene, Leo. Anati, “Inu mukukhulupirira zimenezo?”

Ine ndinati, “Ndi mtima wanga wonse.”

¹²⁴ Iye anati, “Usiku wathawu, nditaima mu msonkhano wanu, M’bale Branham, ine ndinawona kuzindikira za mumtima kumeneko. Ine ndinali ndisanakuwonapo iko nkomwe mu Amerika, mu dziko langa.” Iye anati, “Anthu achi Amerika awa samalidziwa nkomwe Baibulo. Chinthu chokhacho chimene iwo amachidziwa ndi chipembedzo chawo. Iwo samadziwa nkomwe pamene iwo akuima.” Anati, “Iwo samadziwa chirichonse.” Iye anati, “Koma pamene ine ndinaima pamenepo usiku watha,” anati, “ine ndinati...” Tsopano, M’bale Gene, ine ndikungonena izi molemekeza ndi chikondi ndi zotero. Iye anati, “ine ndinati, ‘Ameneyo ayenera kukhala mneneri.’ Koma pamene ine ndikuwona kuti inu mumakhulupirira kuti Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera siinali milungu itatu, zinali zikhumbo zitatu, ndiye ine ndadziwa kuti inu ndi mneneri wa Mulungu, kapena apo izo sibwenzi zitawululidwa kwa inu chomwecho.” Iye anati, “Chimenecho ndi chizindikiro changwiro.” Anati, “Ine sindinayambepo...” Anati, “Inu si Waumodzi?”

¹²⁵ Ine ndinati, “Ayi, bwana. Ine sindine Waumodzi. Ine ndimakhulupirira mwa Mulungu kukhala Mulungu Wamphamvuzonse, ndipo zikhumbo zitatu ndi maudindo atatu chabe amene Mulungu mmodziyo anadzakhalamo.”

¹²⁶ Iye anati, “Adalitse mtima wanu!” Iye anati, “Tsiku lina inu mudzakhetsera magari anu padziko lapansi chifukwa cha zimenezo, koma,” anati, “aneneri nthawizonse amafa chifukwa cha ntchito yawo.”

¹²⁷ Ndipo ine ndinati, “Chotero izo zikhale chomwecho, ngati izo zidzamukondweretsa Ambuye wanga.” Kumasulira kwa Baibulo la Lamsa.

¹²⁸ Oh, ndi zoonza kwambiri. Ndi kangati, monga ine ndimanenera kwa mpingo uno, monga Samueli ananenera iwo asanamusankhe Sauli, “Inu musanatuluke ndi kukajowina chipembedzo chinachake tsopano, ndi kukazimangirira nokha mu mtundu wina wa chipembedzo, bwanji osangowulola Mzimu Woyera kuti uzikutsogolerani inu?” Bwanji inu osamutenga Mulungu kukhala Mtsogoleri wanu ndi kumulola Iye kuti azikudalitsani inu, ndi kuyiwala za chipembedzo chanucho? Tsopano, ine sindikunena kuti inu musakhale wa chipembedzo chirichonse cha tchalitchi, inu mukhale wa chirichonse chimene inu mukuchifuna. Izo ziri ndi inu. Koma ndikukuuzani inu, ngati munthu panokha, mulole Mzimu Woyera kuti uzikutsogolerani inu. Inu muziwerenga Baibulo. Ndipo chimene Baibulo likukuuzani kuti muchite, inu muzikachita chimenecho. Mulungu akudalitseni inu.

¹²⁹ Ndipo tsopano ine ndadikirira nthawi yaitali. Ine ndikudabwa ngati alipo aliyense pano yemwe amafuna kuti abwere kudzadutsa pa mzere wa pemphero kuti adzapemphereredwe. Ngati alipo, angakweze manja awo.

M'modzi yekha, awiri, atatu. Chabwino. Inu nonse mubwere kuno ndipo mudzaima apa ndiye ngati inu mukufuna kutero, pa nthawi ino, ndipo—ndipo tikhala ndi pemphero. Ndipo tikatero ndife...ine sindikufuna kuti inu muchoke pakalipano. Ine ndikufuna kuti ndichite mwadongosolo chinachake pano basi ife tisati—tisanatseke.

¹³⁰ Ndi angati amene akonda kuphunzira kwa Bukhu la Agalatiya... oh, ine ndikutanthauza Aefeso? Tsopano, Lachitatu usiku, ife tidzalowa mu Chisindikizo. Ndipo kenako Lamlungu lotsatira mmawa, tidzakalowa mu kuwuika mpingo pa malo ake. Oh, ngati...mwinamwake ife tidzayambira zimenezu, Lachitatu usiku likubwerali, kwa inu anthu kuno mu Jeff. Kuwuyika mpingo pa malo ake pamene iwo akuyenera kukhalapo, aliyenseyo. Momwe ife timaitanidwira mwa kukhazikitsidwa. Mulungu watikhazikitsa ife kukhala ana, ndife ana mwa kubadwa. Tinakhazikitsidwa ndi kuyikidwa pa malo mwa Mzimu Woyera. Taonani! Aliyenseyo anali Muhebri, pamene iwo ankawoloka mtsinje, koma Yoswa analigawa dzikolo ndipo anampatsa aliyense malo ake monga mwa zoyankhula za amayi ake pa kubadwa, kumene Mzimu Woyera unkamuuza iye.

¹³¹ Tayang'anani pa Yakobo pomwe iye ankafa, mneneri, wochititsidwa khungu, anakokera mapazi ake pa bedi, anati, "Bwerani kuno inu ana a Yakobo ndipo ine ndikuuzani inu komwe inu muti mudzakakhale pa tsiku lotsiriza." Ulemerero! Oh, ine ndikudziwa ndikhoza kuwoneka mwachilendo. Anthu akhoza kuwoneka mwachilendo. Koma, oh, ngati inu mukanangodziwa chi—chitsimikizo, ku—kuyaka kwa mu mtima! "Bwerani kuno ndipo ine ndikuuzani komwe inu muti mudzakakhale mmasiku otsiriza." Ndipo ine ndikhoza kutenga Lemba lomwe lomwelo, ndi kutenga mapu a kumene Ayuda akukhala lero ndi kutsimikizira kwa inu kuti iwo ali pa malo omwewo amene Yakobo ananena kuti iwo akanadzakhala mu tsiku lotsiriza. Ndipo sanachite konse, kumeneko, sanakhale pa malo amenewo kufikira iwo atadzabwerera kuyambira pa Meyi wa seveni, 1946, usiku umene Mngelo wa Ambuye anawonekera kwa ine kumtunda uko ndipo nandiuza kutema uku. Ndipo ine ndikhoza kukuwonetsani inu zimenezu, pamene iwo ankabwerera kupita mdziko latsopanolo, iwo amadzafikira ndendende pa malo amene Yakobo adanena kuti iwo akanadzakhala. Ndipo uko iwo akukhala pamenepo lero. Oh, oh, mai, oh, mai! Ife tayandikira ndi tsiku limodzi kufika Kwathu, ndizo zonse.

¹³² Inu anthu okonedwa, amene mukudwala, kapena inu sibwenzi mutaimirira pamenepo basi kufuna kungoti muime. Ndine m'bale wanu. Ndiri ndi kutuma kochokera kwa Mulungu kuti ndidzapempherere odwala. Osati ngati zanga... ngati kuti ndiri ndi mphamvu yochiritsa, ine ndiribe. Koma ndiri ndi

mphamvu ya pemphero. Monga ine ndinanena mmawa uja, Davide analibe chirichonse koma legeni yaing'ono, koma iye anati, "Ine ndikudziwa chimene iyo iti idzachite ndi mphamvu ya Mulungu pa iyo." Mukuona? Ine ndangokhala ndi pemphero laling'ono lokha kuti ndikupempherereni inu, ndi manja anga kuti ndiwayike pa inu, koma ine ndikudziwa chimene chikhulupiriro mwa Mulungu chichite. Icho chawachitirapo ena, icho chidzakuchitirani inu. Inu muzikhulupirira zimenezo tsopano pamene inu mukunyamukapo, yandikirani pang'ono ku malowa.

¹³³ Tsopano, ine ndikudabwa, kuti ndizipange izi zikhale zokhudza, ngati ine sindingamupemphe m'bale wanga kuti abwere kuno ndi kudzawazodza iwo ndi mafuta. Kodi inu mungachite zimenezo, M'bale Neville? Ine ndiwupemphe mpingo ngati inu mungaweramtse ku pemphero.

¹³⁴ Tsopano kumbukirani, sabata latha pamene ine ndinadwala kwambiri chifukwa cha mafuta akale a msasi aja, ine ndikanakhoza kungololera chirichonse ngati winawake akanati abwere ndikudzaika manja pa ine. Ngati ine ndikanakhala ndi winawake atabwera pafupi, yemwe Mulungu wamudalitsa ndi kumuthandiza, ine ndikanayamikira izo kwambiri. Inu nonse mukumverera tsopano monga mmene ine ndimamverera pamenepo. Inu mukumverera tsopano kuti mukufuna kuti ndikuchitireni monga mmene ine ndimafunira winawake kuti andichitire ine nthawi imeneyo. Mulungu asalole kuti ine ndidzaizembe konse ntchitoyo. Ine nthawizonse, kaya ndatopa, kaya ndalema, pamene ine sindikukhoza kunyamula phazi limodzi kuchoka pa limzake, ine ndizipita, chifukwa ine ndidzakakumana ndi aliyense wa inu kenanso, uko mu Dziko lija kumeneko.

¹³⁵ Ndiye inu akazi okalamba, amuna okalamba, olema, tsitsi la imvi ndi lothothoka, ndipo likuthothoka mzidutswa monga duwa limene latsegula kantibo kake, nkumagwetsa maluwa ake ndi nkumathothokapo, inu mukungosweka mzidutswa, si choncho inu? Ndiko kulondola. Basi...Ndipo chinthu chokhacho chimene inu mukufunira kuti muzikhalapo ndikuti muziwala kwa ulemelero wa Mulungu. Chotero pamene mdani wakumbwandirani inu tsopano ndipo wakuthawitsani, ine ndikubwera ndi legeni ya Mulungu, ndi chikhulupiriro, ndi mphatso imene Mulungu anandipatsa ine. Izi ndi zimene ine ndinanena, kuchitira kuti inu mumvette izi. Ine ndinati, "Ngati Petro atati wangolowa, kapena ena a iwo." Musanene zimenezo. Inu musachite kundipempherera ine. Mungolowa monga chonchi, ndipo mudzanene, monga kwa mkazi uyu, kuti, "Kodi ndinu mlongo *Wakuti-ndi-wakuti?*" Dzina lanu ndi ndani? Mlongo Howard. Kutu, "Ndinu Mlongo Howard. Ndinu wokhulupirira, Mlongo Howard? Mukukhulupirira. Ndinu wokhulupirira. Ndiye, inu mukuona, muli ndi maufulu ku

madalitso onse achiwombolo.” Ndiye ine ndikhoza kunena kuti, “Mlongo Howard, chirichonse chikhala bwino,” ndi kuchokapo. Oh, motani . . . ine ndinati, “Ine ndikhoza kufuula, ndikhoza kukuwa.” Ine ndingati, “Ambuye, zikungoyenera kuchitika. Izo zikungoyenera kuchitika.”

¹³⁶ Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, anthu amaganiza chinthu chomwecho pamene ine ndibwera kuti ndidzawapempherere iwo.” Chotero ndicho chimenecho. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

¹³⁷ Ndipo ine ndaimapo, nthawi zambiri, ndi kuwatenga anthu, ndi kuti, “Oh, mlongo wofunika, kodi inu mukhulupirira Izo? Oh, kodi inu mukhulupirira Izo?” “Ambuye, O Mulungu, apangitseni iwo kuti akhulupirire Izo. Muwapangitse iwo akhulupirire Izo.” “Oh, chonde, kodi muzilandira Izo tsopano?” Si zimenezo ayi. Ine ndinazisiya zimenezo. Ine ndinachokako ku zimenezo.

Ine ndimangonena kuti, “Mlongo Howard, inu ndi wokhulupirira?”

“Inde, ndiri.”

¹³⁸ “Chabwino, Mlongo Howard, ngati ndinu wokhulupirira, ndinu wolandira wa chirichonse chimene Mulungu ali nacho.” Ndipo nkungomugwira dzanja lake. Mwaona, ndikukhulupirira zimenezo. Ine ndamukhudza Mlongo Howard poyika manja anga pa iye. Yesu sananenepo kuti “mukawapempherere iwo,” Iye anati, “Akangoika manja awo pa iwo.” Ndi zimenezotu, ndiye iye nkuchiritsidwa. Iye akhoza kunena kuti, “Chirichonse chikhala bwino,” Mlongo Howard. Ndiye mukhoza kupita kwanu ndipo mukakhala bwino. Mulungu akudalitseni inu.

¹³⁹ Ndinu Mlongo . . . [Mlongo akuti, “Hampton.”—Mkonzi] Mlongo Hampton, ndinu wokhulupirira, sichoncho inu? [“Ndine.”] Ndinu wolandira chirichonse chimene Iye anapereka. Mulungu akhale nanu, Mlongo Hampton. Mupite kwanu ndipo mukakhala bwino tsopano. Yesu Khristu akakuchiritsani inu.

¹⁴⁰ Ndinu Mlongo . . . [M’bale akuti, “Slaughter.”—Mkonzi] Slaughter. Ndizo . . . Ndinu amene tinakupemphererani ku chipatala. Ndinu wokhulupirira, ndiye, Mlongo Slaughter, wolandira wa zonse zimene ife timazipempha. Mlongo Slaughter, mulandire zimene inu mwazipempha, ndipo mukakhale bwino. Mulungu apereka izo kwa inu.

¹⁴¹ M’bale Gene, inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupatsani inu? [M’bale Gene akuti, “Inde, bwana. Inde, bwana.”—Mkonzi] Ndipo Ambuye Mulungu akupatseni inu, Gene, ndendende chimene inu mwachipempha! . . . ? . . .

¹⁴² Ine ndikukudziwani inu. [Mlongo akuyankhula—Mkonzi] Ndinu wokhulupirira, mlongo. [“Oh, inde.”] Ine ndikukudziwani inu. Awa ndi amuna anu pamenepo. Ndi iyeyo amene ndinamupempherera pa foni tsiku lija. Ine

nthawizonse ndimakumbukira zimenezo. Sindinathe kupita ku msonkhano ku Tulsa. Anabwera ku msonkhano. Ndipo Ambuye anamuchiritsa iye, ndinamutumiza iye ku msonkhano. Moimirira wina inu mukumuimirira winawake. ["Mphwanga."] Ndi chinthu cha Chikhristu bwanji chimenecho, mlongo! Mukuona? Iye anadzakhala woimirira ena nayenso. Iye anatiyimirira tonse a ife. Ndinu wokhulupirira ndipo muli ndi ufulu kwa chirichonse chimene Mulungu anachilonjeza. Ndine wantchito Wake. Ndipo mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikukupatsani inu chomwe mwachipempha. ["Ine ndikukhulupirira izo."]

¹⁴³ Bwerani, M'bale Neil. Mulungu akudalitseni inu. Wakhala wabwino modabwitsa kwa inu. Ndinu wokhulupirira. Ndikudziwa inu muli. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu akupatsani inu chirichonse chimene inu mukuchipempha, pakuti ndinu wokhulupirira. Ndipo monga wantchito Wake, kwa inu, m'bale wanga, mu Dzina la Yesu Khristu, ndikukupatsani inu chokhumba cha mtima wanu. Pitani ndipo mukalandire icho. Mulungu akudalitseni inu.

¹⁴⁴ Mlongo Bruce, ine ndikukudziwani inu. Namwino wamng'ono amene anakhula nsana wanga amakudziwani inu. Iye amachokera kumusi uko pafupi ndi Motel JJ, Twin J, kapena chinachake monga chimenecho. Inu muwaimirira ena. Ndipo kodi chokhumba chanu ndi chiyani usikuuno kuchokera kwa Atate anu? [Mlongo Bruce akuti, "Cha inemwini, usikuuno."—Mkonzi] Cha inumwini, usikuuno. [Mlongo Bruce akuyankhulanso] Ndiye, mdani wakugwedezeni inu kuposa momwe dokotala angathere, koma ine ndikukutsatirani inu, ndi legeni. Ndipo mu Dzina la Yesu Khristu, ndikulunjikitsa muvi wa legeniyo pa mwala umene unakalowa mu impsyo zomwe zatsekekazo. Izo zikubwezeretsani inu kwa Mulungu, ku nyumba Yake.

Ife takupemphani Inu, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹⁴⁵ Kodi ndinu bambo a mwamuna uyu, bwana? Kodi ndinu wokhulupirira? [M'bale akuyankhula—Mkonzi] Chophuka mmbali mwanu; mmusi, ndipo kumanzere kwanu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu apereka izo kwa inu, bwana, ndipo monga wantchito Wake?

¹⁴⁶ Ambuye, dzanja ili mwinauwake lachita ntchito zambiri zovuta za m'tsikuli. Wabwera pano ndi cholinga, chinachake choti achichite. Perekani izo, chokhumba cha mtima wake, Atate, pamene ine ndikupemphera mu Dzina la Yesu kuti inu mutero. Amen.

¹⁴⁷ Musati mukaikire. Chophuka chimenecho chisiya kukupwetekani inu mmusi pamenepo, ndipo mukhala bwino. Mulungu akudalitseni inu. . . ? . . .

148 [Mlongo akuti, “Chimapweteketsa mutu wanga ndi kummero kwanga. Chikumapweteketsa nthiti zanga ndikamakhosomola. Ine ndimalephera kuimba. Ine ndikumalephera kuchita chirichonse. Ine...?...Ndipo ndikumalephera kugona mokwanira. Ndikumalephera ngakhale kuchita chirichonse.”—Mkonzi] Ndinu wokhulupirira, sichoncho inu? [“Ndine. Ndine wodzazidwa ndi Mzimu Woyera.”] Ndinu wokhulupirira. [“Ine ndikudziwa kuti Mulungu amakhala mkatimu.”] Ndipo ndinu wo—ndinu wolandira wa madalitso onse awa. [“Ine ndikudziwa. Ndipo ine ndikukhulupirira. Ine ndimakhulupirira mu mapemphero anu, M’bale Branham. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu andichiritsa ine. Ine ndikukhulupirira kuti Iye amayankha mapemphero anu.”] Zikomo inu.

149 Atate, ndikumubweretsa uyu, mlongo wanga, mu mzere wa moto, pa chirikati cha chandamale. Ndipo ine ndikumubwezera iye kwa inu, kuchokera mu zikhadabo za mdani, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

150 Basi ndi momwe izo ziti zidzakakhalire. [Mlongo akuti, “Inde, M’bale Branham.”—Mkonzi]

151 [Mlongo akuti, “...?...Ndiri ndi phapo limene limafa, ndipo limodzi linafa.”—Mkonzi] Opareshoni ya mapapo.

152 O Ambuye, pamene mkazi wamng’ono uyu waimirira apa, chonsecho ali pa kuphukira kwa unyamata, ine ndikumupempherera iye. Ndipo phapo limene limayenera kuti likachotsedwepo, ndipo iye adziwerama, moyo wake wonse. Ndinu Atate athu, ndipo ine ndikulunjikitsa moto wa pemphero pa iye kumene, Ambuye, molunjika kupita ku phapo limenelo. Ndikutumiza pemphero ili mu Dzina la Yesu Khristu. Mulole ilo likakhudze phapo limenelo ndi kulichiza ilo. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumupempha izi. Amenii.

153 Ndinu Mlongo. . . [Mlongo akuti, “Mlongo Gibbs.”—Mkonzi] Mlongo Gibbs. [“Mmutu mwanu momwe, ndipo ndikumamva kupweteka pamenepo.”] Ndendende. Mutu wanu wachotsedwa kwa ine. Ndinu wokhulupirira ndi wolandira wa madalitso onse a Mulungu, Mlongo Gibbs.

154 Ambuye, ine ndikumubweretsa iye kwa Inu, ndi legeni yaying’ono iyi imene Inu munandipatsa ine, monga momwe Inu munamupatsira Davide legeni, kuti aziyang’anira nkhosa za abambo ake. Ndipo ngati mdani abwerapo kutsatira nkhosa, iye sankachita mantha. Iye amatenga legeni yaing’ono iyo ndipo amaitsatira mikangoyo ndi—ndi zimbalangondo, ndipo amabwera nayo nkhosayo. Ili ndi pemphero la chikhulupiriro. Inu munandiuza ine kuti ngati ndingati “ndiwapangitse anthu kuti akhulupirire ndi kukhala owona mtima.” Ine ndikumubwezeretsa Mlongo Gert usikuuno. Ine ndikumulanditsa iye mmanja a mdani. Iye ndi nkhosa Yanu. Ine

ndikumubwezeretsa iye ku khola la Atate, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

¹⁵⁵ [Mlongo akuti, “Mlongo Lowe.”—Mkonzi] Mlongo Lowe. [“Ine ndiri ndi vuto la kuthamanga kwa magari.”] Kuthamanga kwa magari. Ndipo ndinu wokhulupirira, si choncho inu, Mlongo Lowe? Wolandira wa madalitso onse.

¹⁵⁶ Ndiye, Atate Mulungu, ine ndikulinga pemphero ili usikuuno, munga ngati lochokera ku legeni ya Mulungu, pa kuthamanga magari kwa Mlongo Lowe. Ndipo mulole kuti nthawi ina imene dokotala adzamuyeze kathamangidwe ka magari, mulole adzamuyang’ane iye ndi kuti, “Akuyenda bwino tsopano.” Iye adzadziwa chimene chachita izo. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupereka izo kwa iye. Amenii.

¹⁵⁷ [M’bale akuyankhula ndi M’bale Branham—Mkonzi] Inde. Ine ndikanakonda ndikanakhala ndi adadi anga pano usikuuno, ine ndikanawapempherera iwo pompano. Ine nditero kwa anu, anonso. Ine ndikumvetsa.

¹⁵⁸ Atate a Kumwamba, mwamuna amene ali khola wa mnyamata uyu, kuti iye ali pano pa dziko lapansi chifukwa cha iye. Ndipo mwana wake yemwe akukhumba kuti abambo ake abwezeretsedwe; ali kutali uko mu dziko la tchimo, chidakhwa. O Ambuye, ine ndikutumiza pemphero ili ndi chikhulupiriro ndi mphamvu, ndipo ndi zonse zomwe ndingaliponyere nazo ilo, nsangalabwi yang’ono iyi, mu Dzina la Ambuye Yesu. Ine ndikuwuvunga iwo pa mdierekezi uyo yemwe anaika chinthu chimenecho chimene chagwidwa uko. Ndipo mulole kuti icho chichoke. Ndipo mulole iye abwerere motetezeka ku khola, mu Dzina la Yesu. Amenii.

¹⁵⁹ [M’bale akuti, “Mundipempherere ine, M’bale Branham, kuti ndikhale ndi Mzimu Woyera. Ine ndikufuna kuti ndirandire Mzimu Woyera. Ine ndikuyenera kutero. Ine ndiri nacho chokhumba. Ine ndikuyenera kuti ndilandire Mzimu Woyera.”] Inu muli nacho chikhumbo choti muwulandire Iwo. Mukufuna kuti mubwere mu Dziko kumene kuli malonjezo onse. [“Inde.”]

¹⁶⁰ Ndipo tsopano, Ambuye, mnyamata uyu ali kutsidya chabe kwa mtsinje, wamanga msasa ku tsidya linalo, ndipo Yordani akusefukira. Ndipo palibe njira iliyonse kuti iye angawoloke pokhapokha Inu mutampangira njira munga Inu munachitira kwa Yoswa ndi kwa Israeli. Ndipo, Atate, ine ndikukupemphani Inu, ngati wantchito Wanu, mumulole m’bale wathu wofunikira, O Mulungu, mulole iye alowe mu Dziko lolonjezedwa ili, lonjezo ili. Kutu, ku mbali inayo, munga ine ndinatengedwerako usiku wina uja, mundilole ine ndikakhale ndi mwayi womugwira iye ndi kumukumbatira manja anga iye, mu Dziko lina ilo, nkuti, “M’bale wanga wofunika.” Perekani izi, Ambuye. Mulole iye alandire lonjezo la Mulungu, Mzimu Woyera. Amenii.

161 O Ambuye, kwa uyu, m'bale wanga wachisomo; dzanja ili lomwe lakhala lachifundo kwa ine, ndipo landichitira zinthu ine, zimene ziri zosaneneka. Iye akukhulupirira ndipo ali ndi chikhulupiriro. Ndipo tsopano mdani akuyesetsa kuti amugwire uyu, mzangayu: shuga. Ndipo iye akuganiza kuti iye—iye akhoza kumugwira mnyamata uyu. Koma ine ndikumutsatira iye. Ine ndikubwera, kudzamubwezeretsa Wanu yemwe, Ambuye, ndikuvunga mwala uwu ndi chikhulupiriro cholunjika. Mu Dzina la Yesu Khristu ine ndikukantha matenda a shuga awo! . . . ? . . . m'bale wanga. Bwezeretsani nkhoa Yanu yomwe ku khola, Atate, mu Dzina la Yesu. Amen.

[Mlongo Bell akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]

162 O Ambuye, mlongo wathu akudziwa kuti kunenepetsa uku ndi kumeneku, chotero adokotala akuti, ndi chinthu chomwe chidzakupheni inu. “Paundi iliyonse, kulemera kopitirira, kumakuchotsera chaka chimodzi,” monga mwa kalendala ya inshuranse. Ndipo iye akufuna akhalire moyo kwa ulemu ndi matamando a kwa Mulungu. Ndipo palibe dokotala yemwe angachite izi, Atate Mulungu. Izo zangokhala mu—mu dzanja Lanu. Ndipo Mlongo Bell wakhala ali wokhulupirika kwambiri. Ndipo wakhala ali wachifundo ndi womvetsetsa mmayesero, amene akudutsamo. Iye wadutsa mmayesero akuya ambiri. Ine ndikumutsatira iye usikuuno, Ambuye. Ndikubwera kuti ndidzakumane naye mdani ameneyo uko. Ine ndikulunjika ndi kulondolera konse komwe ine ndingalunjike nako. Mu Dzina la Yesu Khristu ine ndikuvungira mwala uwo wachikhulupiriro pa mdani uyu yemwe wamugwira iye. Mulole umubalalitse iye, ndipo umuthamangitsire iye kutali ndi iye, ndipo iye adzakhoze kuti abwezeretsedwenso ku msipu wa mthunzi wobiriwira ndi madzi odikha, kudzera mwa Yesu Khristu. Amen.

Zichitika, Mlongo Bell. Musakaikire basi.

163 Mlongo Spencer. [Mlongo Spencer akuti, “M'bale, M'bale Bill, ine ndimawakonda Ambuye bwino tsiku lililonse lomwe ine ndimakhala moyo. Ndipo ndakhala ndikubwera kuno kwa zaka twente, pa malo ano. Ndipo ndakhala ndikuchiritsidwa pafupifupi chirichonse chomwe chakhala chondivuta ine. Mukukumbukira zonse za izo, ndi . . . ? . . .”—Mkonzi] Ine ndithudi ndikutero, mlongo . . . ? . . . [“Ndipo Iye wandidalitsa ine kwambiri! Ndipo ine ndimamukonda Iye bwino, tsiku lililonse la moyo wanga. Ndikudziwa ine ndiri ndi moyo wopambana mwa Ambuye.”] Ine ndikukhulupirira zimenezo, Mlongo Spencer. [“Ndine wokondwa. Ndine wokondwa! Ngati uwu si Mzimu Woyera umene ine ndiri nawowu, ndine—ine ndikadali paguwabe pa chirichonse chomwe Iye alinacho kwa ine. Ndipo ine ndidzafera paguwa.”] Amen. [“Ndi chimene ine ndikufuna kuti Iye adzachite ndipo ine ndakhala ndikufera pa guwa limodzi ndi Yesu.”] Amen. Mulungu akudalitseni inu . . . ? . . . Amen. [“Ndipo ine ndikuuuzani inu chimene ine

ndikufuna kuti inu muchite. Inu mukudziwa, Nowa anatenga banja lake lonse limodzi ndi iye, ndipo ine ndikufuna banja langa lonse. Inu mukudziwa ine ndikufuna okonedwa anga apulumutsidwe.”] Ine ndikumvetsa. Ana anu. Uko nkulondola. [“...?. . .ana anga.”] Inde, amayi. [“Ndi amuna anga.”] Inde, bwana, ine. . . [“Monga momwe inu mukudziwira zonse za izo.”] Inde. [“Inu munatipempherera ife.”]

¹⁶⁴ Ife tonse tikumudziwa Mlongo Spencer, ndipo tikudziwa momwe iye ndi M'bale Jess atsalirabe kudutsa mu zowawa, koma iwo akhala akubwera ku tchalitchi kuno. Pamene ine nditi ndidzawolokere ku tsidya linalo, iwo samadzakavutikako monga chonchi. Iwo adzakakhala achichepere. Oh! M'bale Jess, ngati ine ndikanangoti. . .?. . .inu mukudziwa. Ndiyeno inu nonse mukudziwa momwe, basi—kungowoloka pang'ono. . .?. . . kutsidyako, inu mukabwerera kukakhala mtsikana wamng'ono kachiwiri, ndipo M'bale Jess akabwereranso kukakhala mnyamata wamng'ono. Mulungu anakulonjezani inu.

¹⁶⁵ Tsopano, taonani. Ine ndikufuna kuti ndikupatseni kuphunzitsa pang'ono chabe, pokhala kuti ndinu womalizira pano, ine ndikufuna kuti ndikupatseni.

¹⁶⁶ Chifukwa, ine ndikudziwa uyu ndi mnyamata wanu wamng'ono, Charlie. Inu mukufuna kuti iye apemphereredwe? [M'bale Charlie akuti, “Inde.”—Mkonzi]

¹⁶⁷ Ine ndikufuna kuti ndinene chinthu chimodzi ichi. Kodi munayamba mwawerengapo mu Lemba pamene Baibulo linanena izi? Paulo anamuza Kenturiyo wa Chiroma.

Inu mukukhoza kundimva ine bwino bwino? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]

¹⁶⁸ Anamuza wa Chiroma, pamene iye anasolola lupanga lake, kuti adziphe yekha, uko ku Filipi pamene iye anali mu ndende. Ndipo chivomezi chinagwedezera ndendeyo pansi. Iye anati, “Ukhulupirire pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo iwe ndi nyumba yako mudzapulumutsidwa.” Kodi inu munayamba mwamvapo zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi] “Iwe ndi nyumba yako.” [“Ameni.”] Tsopano, taonani. Ngati iwe uli ndi chikhulupiriro chokwanira cha chipulumutso cha pa iwemwini, kodi iwe sungakhale nachonso chikhulupiriro chokwanira cha pa nyumba yako? [“Ameni.”] Mulungu, mwanjira inayake, achita izo.

¹⁶⁹ Ndipo, Ambuye, ine ndikumupempherera Mlongo Spencer ndi M'bale Spencer, usikuuno, kuti mwana aliyense, iwo ndi ana awo, onse akakhale mu Dziko laulemerero, lokondwa ilo kumeneko kumene sikukakhalako matenda kapena ukalamba, kopanda chisoni kapena zokhumudwitsa, ndipo moyo wonse wawung'ono uwu pano udzazimirira mu maloto amene anadutsa. Mulole iwo alandire ichi, ndipo mulole ana ake onse, ndi mwamuna wake, okonedwa ake onse, ndi onse amene

amamukonda iye, ndi onse omwe iye amawakonda, mulole iwo akakhale kumeneko ndi iye, mu Dzina la Yesu. Amenii.

¹⁷⁰ [Mlongo Spencer akuti, “Amenii. Zikomo inu.”—Mkonzi] Mulungu akudalitseni inu. [“Ine ndikhala eyite-thuu, posachedwapa.”] Zaka eyite-thuu zakubadwa. [“...?...?...” Koma iwo amafooka, akafika usinkhu umenewo. Koma ine ndikumachitabe zophika zanga, kuchapa ndi kusita, ndi kukonza m’nyumba.”] Basi monga momwe dziko likupasukira, Mlongo Spencer. [“Inde, ndi choncho. Ndikumakhala wotopa kwambiri, nthawi zonse. Iwo amakhala nazo izo...Ine ndinawafunsa amayi anga, amayi anga ondipeza, omwe anali ndi zaka nainte zakubadwa, momwe iwe umamverera pamene iwe ukukalamba, kalekale. Iwo anati, ‘Rose, mwinamwake iwe umakhala wotopa nthawi zonse.’ Ine ndatopa.”] Chabwino, iwe umangokhala kuti wakonzekera kuti uzipita kukapumula, inu mukuona. [“Ine ndimakhala wotopa kwambiri, nthawi zonse. Ine ndikufuna nditakapumula. Ine ndikusowa chimenecho.”] Inde, mayi. [“Ndipo ine ndikufuna kuti ndikapumule mwa Ambuye, pansa pa mawondo anga. Chonse, chirichonse chimene ine ndikuchisowa.”] Inde. Ingosungani chikhulupiriro chanu molondola pa Iye, Mlongo Spencer, ndipo inu mudzawolokerako. [“Ine ndikufuna ndidzafere paguwa, mu Dzina la Yesu. Ndi amene ine ndimafuna nditakamuwona, kufikira Iye akamaitanabe.”] Ndipo Iye anati... [“Ine ndikufuna chirichonse chimene Iye wandisungira ine.”] Ndipo motsimikiza basi monga momwe ine ndaimira pano chomwechi ndi inu, usikuuno, Mlongo Spencer, mwa chisomo Chake ine ndidzakakuwonani inu ndi Jess kutsidya linalo, wamng’ono ndi wathanzi. Inu nonse mudzakhala mukuthamangirako, mukufuula, “M’bale wanga! M’bale wanga!” [“Inde.”] Inde ndidzakakuwonani inu.

Manjenje ake.

¹⁷¹ Atate Mulungu, mtsikana uyu anali ndi kusokonezeka, ndipo iye wadutsa poti mankhwala sangamuthandize. Pali iye yekha, amene akulepheretsa. Koma ine ndikumubwerera iye usikuuno. Ine ndikubwera kwa Inu, Atate. Ine ndikubwera, kudzakupemphani Inu kuti mulondelere chipolopolo chimene ine ndikuyenera, kuchiwombera. Mulole icho chiwombere molunjika, tsitsi lolukana kumbuyo kwake. Mulole pemphero ili, mu Dzina la Yesu khristu, likakanthe manjenje amenewo ndipo likawakhadzulire iwo mzidutswa, ndikubwezeretsa nkhoa iyi ya msipu wa Mulungu. Amenii.

Zikungoyenera kutero, wokondedwa.

¹⁷² [Mlongo akuti, “Mungopemphera. Ine ndiri ndi ana sikisi amene ine ndikumupempha Mulungu kuti awachiritse ndi kuwapulumutsa.”—Mkonzi]

¹⁷³ Mulungu wa Kumwamba, perekani zimenezo, ana ake sikisi amene iye akukhumba kuti apulumutsidwe. Iye wamva

umboni uja wa M'bale Daulton, ana ake aakazi okonededwa. Iye akuwakhumba ana ake sikisi, Atate. Mulole iye akhale nawo iwo. Mulole iye adzakakumane nawo iwo mu Dziko ilo kumene kulibeko usiku, otetezeka bwino ndi ophimbidwa ndi Magazi a Yesu Khristu. Amenii.

Mukhale nawo iwo, mlongo, pemphero langa.

[Mlongoyo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi]

¹⁷⁴ Ine ndikukukhulupirirani inu. Palibepo chirichonse, nkomwe, chomwe chingathandizire izo. Iwo awapatsa iwo kanthu kakang'ono komwe kakuwoneka ngati, oh, chinachake ngati acetamin. Ndi cortisone, iwo amawatcha iwo. Awo, awo amakupha iwe, pafupifupi. Iwo amabalalitsa magazi ako kwambiri. Koma, taonani. Mukuona, nyamakazi imakhala ngati mkango umene unagwira nkhosa ndi kuithawitsira iyo kutali. Tsopano, kodi legeni ingachite chiyani? Oh, mai! Apo pali mkango waukulu, wobangula uli ndi mwanawankhosa. Ndipo iwo umakonda mwanawankhosa, chotero iwo wathawa naye mwanawankhosa. Koma Davide anatenga legeni ndipo anawutsatira iwo. Mukuona? Tsopano penyani. Iye anali ndi miyala faifi: f-a-i-t-h, iyemwini, m-w-a. Legeni yake inali m'dzanja *ili*: J-e-s-u-s. Iye amagenda mwakupha. Chinachake chikuyenera kuchitika. Tiyeni tiitsatire nyamakazi imeneyo, usikuuno, mwa pemphero ili. Mulungu apereke izo kwa inu.

¹⁷⁵ [Mlongo akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi] Iye akufuna kuti abatizidwe mu Dzina? ["Ayi. Ayi. Iye sananene zimenezo."] Inu mukufuna kuti iye abatizidwe. ["Ndi khumbo langa kumuwona iye atabatizidwa."] Zikomo inu, mlongo. Osati chifukwa chakuti imeneyo ndiyo njira yake. Ndi chifukwa chakuti... Tsopano, ngati zimenezo zikanakhala mu Baibulo, za, "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera," ine—ine ndikanakhulupirira izo, ine ndikanakhala pomwepo ndi izo, mlongo. Ine—ine sindikanafuna kuti ndikhale wosiyana mulimonse. Ine—ine ndikanafuna kukhala chomwecho. Ine sindikanalola... ine—ine ndikayankhira zimenezo, inu mukuona. Ndipo ine ndikuyenera kunena izo basi m'mene *Ilo* likunenera izo; osati kuti ndikhale wosiyana, koma kuti ndikhale wowona mtima.

¹⁷⁶ Tsopano, Atate, ife tikutsatira okonededwa ake omwe ali ndi nyamakazi, ndipo apa iye akufuna kuti iye abatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu, pakuti pamenepo ndipo polowera pake. Ndicho chipata chotseguka. Ndi pamene Yoswa anatsegulirapo njira imene imawolokera kupita ku dziko lolonjezedwa. Panalibe malo awiri kapena atatu amene anatsegulidwapo; analipo amodzi okha.

¹⁷⁷ Petro, pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mpingo unayambitsidwa koyamba, anaitsegula njira, anati, "Lapani aliyense wa inu ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu

Khristu.” Iwo sanachokeko nkomwe pa njira imeneyo, aliyense anawolokerapo kupita ku Dziko lolonjezedwa.

¹⁷⁸ Ena a iwo amayesetsa kuti awoloke, kumusi komwe uko kudzera pa kamtsinje kena, ndipo Paulo anati kwa iye, “Kodi inu munabazidwa ku chiyani? Kodi inu mukuyesera kuti muwolokere pati?”

Ndipo iwo anati, “Kumusi kuno kumene Yohane anayang’anako.”

¹⁷⁹ Iye anati, “Chabwino, Yohane amangokulozerani inu ku nthawi, ndi malo.” Ndipo kenako pamene iwo anamva ichi, iwo anabatizidwa pa mtsinje woyenera. Ndipo iwo anawoloka, ndipo anakalandira mpesa wa Mzimu Woyera.

¹⁸⁰ Perekani izi kwa mlongo wathu ndi okonedwa ake, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹⁸¹ M’bale Lyle. [M’bale Lyle akuti, “Ine ndikukhulupirira kuti ndithudi ndinu bwana woyenera, M’bale Branham.”—Mkonzi] Oh, m’bale! [“Munayendapo . . . ? . . . Inu mukukumbukira ngati pakanakhala kuti mu loto, panabwera chinachake . . . ? . . . Ngati inu mulitchule lotolo, izo ndi zabwino. Awo ndi amene ine ndinali nawo. Chimene, inu nthawizonse mwakhala mukulota molondola! . . . ? . . .”] Inde. Apo ndi pakale. [“Inde.”] Inde. Ndine wokondwa . . . ? . . . Mulungu akudalitseni inu. Inu muli paulendo wopita ku Dziko lolonjezedwa tsopano! Mwinamwake ine ndichitchula chimenecho.

¹⁸² Ndi angati akukumbukira basi utumiki uwu usanatsimikiziridwe kwa ine, ndipo ine ndikuwedza ndi munthu tsiku lina, kumusi kwa mtsinje uko, ku nyanja? Ndipo ine ndimagwira nsomba zing’onozing’ono, ndipo Mzimu Woyera unabwera pa ine. Apo panali a . . . Bambo uyu ndi wa Mboni za Yehova, anali. Mchimwene wake ali pano penapake, Banks Wood. Iye ali muno penapake, yemwe ali woyandikana nane wanga.

¹⁸³ Uyu ndi Lyle. Ndipo anthu awa anali a Mboni za Yehova. Ndipo iwo anati, tsiku lina pamene ife tinkawedza kumusi uko, mnyamata uyu atatembenuka, ine ndinamuza iye kuti muli chinachake mmoyo wake, ndi chimene—chimene chinadzachitika, ndi zonse za izo. Zimene, iye wangondiiza kumene ine, ndipo tsopano wangozichotsamo izo mmoyo mwake, uko nkulondola, zonse zomwe izo zinali. Zinali zolondola ndendende. Abambo ake ndi amene anali wo—wowerenga. Kodi adadi ali pano usikuuno, Billy? [Winawake akuti, “Sindikudziwa.”—Mkonzi] Ndipo iye ndi mkazi wake, awiri onsewo, anabatizidwa, kuchitira umboni mu Dzina la Yesu Khristu, kuno mu dziwe. Ndipo mwamuna uyu anakhala pafupi ndi ine, tsiku lina.

¹⁸⁴ Banks, ulikuti? Kodi iye ali pano usikuuno? [Winawake akuti, “Kumbuyo komwe uko pa ngodya.”—Mkonzi] Kumbuyo pa ngodya. Inde.

¹⁸⁵ Ndipo ife tinali tikuwedza. Ndipo, m’bale, mnyamata wanga wamng’ono anali atapha... Ine ndimaganiza kuti iye anali atapha kamphaka, masiku angapo mmbuyo mwake. Mphaka wa kholo wokalamba uja anali ndi gulu la tiamphaka, ndipo anakanyamula iko ndipo anakagwetsa iko. Ine ndinaganiza... ine ndinati, “Ambuye awukitsa moyo wawung’ono,” dzulo lake. Nkulondola uko, Lyle? [M’bale Lyle Wood akuti, “Inde.”—Mkonzi] Atakhala uko ku una. Ndipo ine ndinati, “Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE.” Ndipo ife tinawedza usiku wonse ndipo sitinagwire kalikonse.

¹⁸⁶ Mmawa wotsatira, ife tinali kuwedza, mmbuyo mu una waung’ono, kuti tipeze ndunduma. Imeneyo ndi nsomba yaing’ono. Ndipo M’bale Lyle anali ndi mtengo waukulu, ndipo iye anaisiya kuti ndunduma yaing’onoyo imeze iyo, mbedza yaikulu yomwe iye anali nayo, mpaka, pamene iye anaikokera iyo panja, kachingwe kakang’onoko konse kanali kali pansi, mbedza yaikuluyo, m’mimba mwa ndunduma yaing’ono. Ndipo pamene iye amaikokera iyo panja, iye amangoyenera kuti akokere panja matumbo onse ndi chirichonse kuchokera mu ndunduma yaing’onoyo, kuti aigwire iyo. Ndipo anangoikokera iyo panja, chifukwa mbedza yaikuluyo inali itakodwa m’mimba mwa nsombayo. Ndipo pamene iye anatero, anaiponyera iyo pansi mmadzi. Ndipo iyo inangonjenjemera, kanayi kapena kasanu, ndipo basi zinathera pomwepo, chifukwa matumbo ake ndi makha ake anali akulendewera kunja kwa kamwa yake. Ndipo iyo inayandama pamenepo kwa pafupifupi theka la ora, inadzayandamanso kubwerera pa timaudzu.

¹⁸⁷ Ndipo ine ndinali nditakhala pamenepo, ndikuwedza. Ndipo mwadzidzidzi, Mzimu Woyera unabwera, unati, “Yankhula kwa nsomba imeneyo.”

¹⁸⁸ Ine ndinati, “Nsomba yaing’ono, Yesu Khristu akukupatsanso iwe moyo wako.” Ndipo nsomba yaing’ono iyo, itagona yakufa mmadzi, inadzitembenuzira mbali yake ina, ndipo inangoti ruuuu, kukalowa m’madzi, mwaliwiro basi monga momwe iyo ikanathera.

¹⁸⁹ M’bale Lyle ndi M’bale Wood anali atakhala pamenepo. M’bale Lyle anati, “M’bale Branham, izo zinali za ine, chifukwa ine ndinanena kwa yaing’onoyo... .

¹⁹⁰ [M’bale Branham akuyankhula ndi M’bale Lyle Wood—Mkonzi] Usikuuno, ine ndikhoza kuwauza iwo zomwe inu munanena? [M’bale Lyle Wood akuti, “Inu ndithudi mukhoza. Ziri bwino, M’bale Branham.”]

¹⁹¹ Iye anati, pamene iye anatulutsa matumbowo mwa iyo, anaiponyera iyo pamenepo, anati, “Iwe wawombera chipolopolo

chako chomaliza, mzanga wamng’ono,” basi monga chomwecho. Anaiponyera iyo panja.

Iye anati, “Izo—izo zimatanthauza ine.”

Ndipo ine ndinati, “Ayi, M’bale Lyle. Sizinali zimenezo.”

¹⁹² M’bale Banks kumbuyo uko, anati, “Ndi anthu angati mdziko lino, ndi masauzande angati, omwe angakonde kuima pamene ife tikuima pakali pano, kuti awone mphamvu ya Mulungu ikutsika ndikudzachita chinachake monga chimenecho!” Mwakuyankhula kwina, iye anali ngati. . .

¹⁹³ Ine ndikukhulupirira ife tonse tinamverera monga momwe Petro anachitira, “Ndi zabwino kukhala pano. Tiyeni timange makachisi atatu.” Mukuona? Uko nkulondola.

¹⁹⁴ Tsopano, M’bale Lyle, iwe wadzozedwa ndi Mzimu Woyera tsopano. Wachoka ku Igupto. Miphika ya gariki ndi nyansi za mdziko zatsalira mmbuyo. Iwe waima pa gombe la Yordani tsopano, basi kutsidya ilo. Mulungu akuwolotsere iwe kumeneko; Lyle.

¹⁹⁵ Mulungu Wamphamvuzonse, apa pali chikho Chanu. Iye ndithudi anali mu kuzingwa kowopsya, Ambuye, koma mtima wanga unamutsatira iye. Mapemphero athu anangokakantha chibhakera chopangitsa nyenyezi kumeneko, ndipo chinthu kumene chimene chimamumanga iye chamuchokera iye. Icho chaswedwa. Ndipo tsopano akuyenda kutsikira ku Yordani. [M’bale Lyle Wood akuti, “Zikomo Inu, Yesu.”—Mkonzi] Mtengereni iye ku Dziko lolonjezedwa, Ambuye. [“Inde, Ambuye.”] Ndipo mukamusindikize iye pakati pa anthu. [“Inde, Ambuye.”] Kuti, pa Tsiku laulemelo limenelo pamene ife titi tidzakakumane kutsidya, mundilole ine ndidzamverere kukumbatira kwa mikono yake, akufuula, “M’bale wanga wofunika!” [“Ameni.”] [“Ine ndikumudziwa Iye.”] Mumubweretse Banks limodzi ndi iye, Ambuye, mutero Inu? Bambo ndi mayi, ndi onse a iwo, chemwali, ndi banja lonse lalikulu ilo, mulole ife tonse tidzakakumane kutsidyako, Ambuye, ndipo mmodzi aliyense wa iwo adzazidwe ndi Mzimu Woyera. Ine ndikupemphera mu Dzina la Yesu. Ameni. [“Ameni.”]

Ine muwulandira Iwo, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, M’bale Lyle.

¹⁹⁶ [Winawake akuti, “M’bale?”—Mkonzi] Inde, m’bale. [“Pali foni imene ikuchokera kutali, ndi imfa, akudikirira pa lanya.”]

¹⁹⁷ Pali winawake akufa, pa foni yochokera kutali. Ndipo ndipereka msonkhano kwa M’bale Neville ndikapita m’menemo.

¹⁹⁸ [M’bale Neville akuti, “Tsiku lopambana ndi lalikulu mwa Ambuye! Mulungu watichitira zinthu zina zopambana kwa ife lero. Ziyembekezo zanga zakwaniritsidwa kwathunthu.”—Mkonzi]

[“Tiyeni tiime pamodzi, pa mapazi athu.]

199 ["Mukumbukire msonkhano ndiye, Lachitatu usiku. Mukhale mukupemphera kwambiri. Mitima yonse yosakhutitsidwa, yosatsimikiza ilumikizane kwambiri ndi Mulungu. 'Nthawi yayandikira. Nthawi yake ndi ino. Lero ndiro tsiku la chipulumutso.']

200 ["Mulungu adalitse aliyense wa inu alendo, anthu inu amene mukuchokera kutali. Pemphero lathu ndi lakuti Mulungu akupatseni inu zifundo za mayendedwe, kubwerera kumene mumakhala. Zinali zabwino kuti tinali nanu limodzi nafe. Ndipo muzitipempherera ife pamene mukupita, kuti Ambuye adalitse pa malo ano, aponso.].

201 ["Atate Athu Akumwamba, monga wantchito Wanu wabwera usikuuno, kudzagwira ntchito ya mu ofesi ya wantchito Wanu ndi mneneri, kudzaimirira pakati, padanga, akupanga lingalo, akubwera kwa ife ndi chikhumbo choyaka cha wantchito Wanu, monga kubatizidwa ndi Mzimu Woyera, ndi kupatsidwa ofesi ya mneneri, kuti adzayankhule kwa kam'badwo kano. Mutithandize ife lero ndi usikuuno, kuti tilandire Uthenga umene ukubwera kwa ife, Ambuye, chirimbikitso, kuti tikhale okonzeka.].

202 ["Mumudalitse wina aliyense amene azidutsa pa makomo a nyumba iyi usikuuno. Mulole matenda omwe ali pa ife, omwe ife sitikudziwa kalikonse ka iwo, mulole chisomo Chanu chodala ndi mphamvu zitisamalire ndi kutitetezera ndi kutichiza ife, ndi kutisunga ife, kufikira nthawi imeneyo pamene Inu mudzakhale wokonzeka kuti mutisamutsire ife kupita ku mbali inayo. Mudalitse onse ogwetsedwa ulesi ndi okhumudwitsidwa, amantha, ndi iwo amene ali ofooka.].

203 ["Mulungu, ife tikupemphera usikuuno kuti mutiyendere mwapadera, kudalitsa kwa Mzimu Woyera, kuti kukhale pa wapaulendo aliyense, mwendamnjira aliyense, mlendo aliyense amene ali pa zipata zathu. Aliyense yemwe ati atuluke pakhomo usikuuno, mulole chotchinga icho cha Magazi, ochokera pa mtanda wa Kalvare, aphimbe mokwanira ndipo apereke.].

204 ["Mukatichize ife pamene tidwala. Mukatisunge ife pafupi ndi mphamvu Yanu yaikulu. Mutidzozere ife ku utumiki. Mutilole ife tikayende mu chikondi, pamaso Panu, masiku onse a moyo wathu. Ndipo ife tidzakutamandani Inu chifukwa cha izi, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu Khristu ndi chifukwa cha Iye. Amenii.].

205 ["Ndipo Mulungu akudalitseni inu. Ndipo ndife okondwa kuti tinali ndi inu. Gwiranani chanza wina ndi mzake."]

206 [M'bale Branham akubwerera pa nsanja pamene osonkhana akugwirana chanza ndi kulonjerana wina ndi mzake pamene akunyamuka.].

207 [M'bale Branham akuyankhula ndi winawake.]. Ndikuyamikira kwenikweni zonse zimene inu mwandichitira

ine, khadi ndi...?....Inde, bwana. Ndikuyamikira kwenikweni...?....

²⁰⁸ [M'bale Branham akuyankhula ndi M'bale Neville—Mkonzi.] Chotero ife tinatumiza mwala wa chikhulupiriro...?....Panali mwamuna wochokera konkuno...?....Chotero ine ndinatumiza pemphero lomutsatira iye, mu Dzina la Yesu Khristu. Wakhala atagona pamenepo kwa ora, osagunda, osapuma, osapanga chirichonse. Osapuma, osagunda, osatulutsa mpweya, osapanga chirichonse; maso atakhala pa mutu wake, anadzagwera paguwa. [M'bale Neville akuti, "Iye anangomusiya agone pamenepo kufikira pemphero limenelo litabwerapo."]

²⁰⁹ Kodi *ichi* chikadali chotsegulabe? [M'bale Neville akuti, "Inde, ndi choyatsabe," akulozera kuti maikrofoni akadali oyatsabe—Mkonzi]

²¹⁰ Kodi ndingakhale ndi tcheru chanu? Kuntunda uko, mvangeri wamng'ono, mlaliki, kuno ku Indiana, amalalikira, anadzagwa ndi kufera paguwa, pafupifupi ora lapitalo. Pamene iye amalalikira, anagwa chafufumimba, ndipo anafera paguwa, mvangeri wodziwika, amalalikira kuno ku Indiana. Abusa anangobwera ndipo anadzandiimbira ine. Iye anafa pamene amalalikira pansu pa kudzoza kwa Mzimu, anagwa chafufumimba, maso ake okhazikika, kupuma kwake kunamuchokera iye. Iye analengezedwa kuti wafa, wakhala atafa kwa ora. Ndipo chinachake chinawauza iwo kuti ayimbire ku tchalitchi ndi kundipempha ine kuti ndipemphere. Chotero ine ndinatumiza pemphero kuti limubweze iye, mu Dzina la Ambuye Yesu. Mulumikizane nane mwa chikhulupiriro, kuti lisaphonye chandamale; limutsitsimutse iye ndi kumubwezeretsanso iye. Zikomo inu.

²¹¹ Mulungu akhale nanu, mpaka ndidzakuwoneninso inu Lachitatu usiku. Inu anthu ochokera ku Georgia ndi kozungulira, bayi-bayi. Mulungu akhale nanu.

²¹² M'bale Pat...?....



KUKHAZIKITSIDWA 1 CHA60-0515E
(Adoption 1)

MAULALIKI A KUKHAZIKITSIDWA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu usiku, Mei 15, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org